


# MAFUNSO NDI MAYANKHO

 Usiku wabwino, abwenzi. Ine ndinali kungoyankhula naye m'busa wathu wokonedwa, m'bale. Ine ndiri... ine ndikulingalira panali zina zoyikidwa pambali zimene ine sindinazifikire; ine sindikanatha basi kupita patsogolo penanso. Mai, ine ndiri wong'ambika kwambiri ndi masomphenya. Mukuona? Ndipo iwo akhala ali ambiri, pafupi fifitini kapena twente madzulo awa, ndipo iwo basi akungonding'amba ine mu zidutswa. Ndimangowona malo aang'ono kwambiri apa ndi apo. Ine ndimatuluka umo; ine ndinati, M'bale Neville, n—ngati inu mungathe kupitirira nazo, pitirirani nazo; ine ndikufuna kuti ndizembe ndi kupita kunyumba.” Ine ndinati, “Ine ndatsala pang'ono kuti ndigwe, ngakhale mtima wanga ukagunda, kulumphu.” Ndipo ine ndinati, “I—ndiri... basi ine sindingathe kuima mopitiriranso.”

<sup>2</sup> Iye anati, “M'bale Branham, anthu akhala akundifunsa ine ngati inu mukanati mutsirize kuyankha mafunso aja.” Ndipo i—i—ine sindimafuna nkomwe kuthawa pa mzere wa ntchito. Ine ndikumuyamikira M'bale Neville. Ndipo mwinamwake kwa maminisi apang'ono ine ndichita mopambana momwe ine ndingathere. Ndipo i—ine ndikudziwa pali... Billy anabwera mkati umo; ine ndinati, “Kodi iwe unawatenga iwo onse?”

<sup>3</sup> Iye anati, “Ababa, pali twente kapena ochulukira amene ali chiyimire—akuyembekezera.” Kotero ine sindikanatha kuwatenga... Amenewo ndi anthu ena sate achilendo lero, ndi pafupi masomphenya twente-faifi a iwo; chotero inu mukhoza kulingalira pamene ine ndaima. Kotero i—ine ndiri wotopa kwenikweni, wotopa kwenikweni mwaubongo. Koma ife tipemphera, nkuyamba nawo kumene mafunso awa pamene ife tinasiyira. Ndiyeno, pamene i... Ngati ine ndipita ku Arizona ndi izi ziri mu malingaliro mwanga, ine ndikakhala ndikuvutitsidwa nazo nthawi yonse. Ine ndikhala ndikubwerera posachedwa kwambiri, Ambuye akalola, ndi kudzayankhula pa phunzirolo tsiku lina mwamsanga momwe ndingathere, pa kulondola kwa chikwati ndi chilekano. Tiyeni ife tipemphere.

<sup>4</sup> Wokonedwa Mulungu, Inu mukuwudziwa mtima wanga, ndipo Inu mukukudziwa kumverera kwanga; Inu mukudziwa zonse za ine. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, pali anthu ambiri... Ine ndinangowasiya iwo apite nao motalika kwambiri, Ambuye; pali zochuluka kwambiri za izo. Koma ine ndiri woyamikira kwambiri kuti ine sindikukhulupirira kuti panali mmodzi amene anabwera umo lero koma amene anathandizidwa. Ine ndikukhulupirira aliyense wa iwo anatuluka ali wokondwa ndi wokhutitsidwa. Zinthu zimene ine sindikanatha kuziyankha mwiniwanga, Inu mumabwera apo

mu masomphenya ndi kudzawulula mobwerera mu miyoyo yawo (iwo akhala apa, ambiri a iwo, pakali pano akumvetsera kwa izo ndipo akudziwa kuti izo ndi zoono), ndipo mwaullulira kwa iwo zinthu zimene zinali mmbuyo mu moyo zimene zimapangitsa zinthu kuti zizichitika. Iwo akudziwa, Ambuye. Palibe njira mdziko kuti ine ndidziwire zimenezo kunjira kwa thandizo Lanu.

<sup>5</sup> Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti ngakhale ine ndiri wotopa, koma ine ndiri wokondwa kukhala ndiri wantchito Wanu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse awo amene ali modikira, ambiri a iwo amene amafuna kuti alowe muno. Ndipo i—i—ine ndikudalira, Mulungu, kuti iwo akhala—iwo afika posamaliridwa, Mzimu Wanu Woyera waukulu upereka kwa iwo chirichonse chimene iwo ali nkuchisowa.

<sup>6</sup> Ndithandizeni ine kuti ndiwatsirizitse mafunso awa, wokondedwa Mulungu, kapena ndichite mwakupambana momwe ine ndingathere ndi iwo, kuti anthu anu akhale ndi mafunso awo atayankhidwa. Ine ndinawapempha iwo kuti awalembe awo. Iwo anawalembe awo, ndipo ine ndikumverera kukakamizidwa kuti ndiyesere kuwayankhira iwo amenewo. Koteri ine ndikupemphera kuti Inu mundipatse ine mphamvu kuti ine ndithe kuchita ntchito yanga kwa Inu ndi kwa anthu. Mu Dzina la Yesu ine ndikupemphera. Amen.

<sup>7</sup> Tsopano, ife tiyambira apo pomwe pamene ife tinalekezera mmawa uja. Zina za izi ine mwinamwake sinditha kuti ndiziwerege, chifukwa chakuti. . . ine ndasasa mau pang'ono, chifukwa ine ndakhala ndikuyankhula mochuluka kwambiri. Ndi angati amene anali pa zakudziwa za mmitima lero amene akuyamikira Mulungu kwenikweni pokupatsani inu zimene. . . ? Mukuona? Ndizo zopambana za zonse zake, ndiwo mautumiki a mtundu umenewo. Zinthu zimene inu mumafuna kuti muzidziwe ndi zinthu zimene zakhala zitabisika mu moyo zaululidwa ndi kuuzidwa.

<sup>8</sup> N—ndipo kumbukirani, zambiri za zinthu izi. . . Tsopano, ambiri a inu mukudziwa kuti panali ndithudi zinthu zochititsa manyazi zimene zinanenedwa ndi kutulutsidwira kunjira, koma palibe amene akudziwa zimenezo kupatula ine ndi Mulungu. Ndipo zimene zinazidwa kwa inu, zimenezo ziyenera kukhala pakati pa inu ndi Mulungu; mungozisiya izo zokha. N. . . Ndi angati a inu mukudziwa kuti Ambuye anawulula zinthu zimene zinali. . . zinachitidwa kuti zikupatseni inu thandizo? Kwezani manja anu ngati izo zinatero. Mukuona? Popanda kuwadziwa ngakhale anthuwo, popanda kalikonse ka iwo, koma I—Iye anzichita izo.

<sup>9</sup> Tsopano, tiyeni tifique ku mafunso mofulumira ndithu momwe ife tingathere tsopano ndi kuwona ngati ife tingathe kutenga. . . Pali linalake apanso limene liri pano penapake. Ilo

lati, “Nambala firii.” Ine ndikukhulupirira iyi ndi kalata; ndiko kulondola, ndi kalata chabe. Ine ndikupepesa. Ine ndiziika izi apa pamene ine ndikufika kwa izo, ndipo ine ndikuganiza... Inde, bwana, iyi ndi kalata nayonso. Ndipo iyo ikuti, “Funso,” koma ine ndikukhulupirira iyo ndi kalata, funso mu kalata. Ayi, sichoncho, ndi funso la loto. Chabwino, ine ndiwerenga lotolo, ndiyeno ine ndiwona ngati Ambuye ati andipatse ine kutanthauzira kwa ilo, ndi kuzipereka izo kwa inu basi momwe ine ndingathere. Ine ndikulingalira kuti inu muli nayo adiresi yanu. Tiyeni tiwone ngati iyo ilipo; ngati iyo palibe, ine ndikupemphani inu kuti muikepo adiresi yanu, munthu wa funso ili n—ndi loto. Ayi, inu mulibe iyo.

<sup>10</sup> Aliyense amene analemba kalatayi (iyo ili...iyo inangolembedwera kwa ine), mumupatse Billy adiresi yanu, kuti pamene ine ndizipita panjira yanga waku Arizona, ine ndikapita mu chipululu ndi kukapemphera. Ndipo ngati Iye andipatsa ine kutanthauzira, ine ndidziwa koti ndilembereko izo (inu mukuona? Popanda iyo pamenepo kuti ndiperekeko kutanthau-...) ngati Iye apereka iko. Koma ine sindinena izo kupatula izo zitatero, chifukwa ine ndingakhoze kuchita izo zokha; ndiye ine ndidzadziwa kuti izo zikhala ziri zolondola. Tsopano.

**376. Kodi Mkwatibwi, awo amene akukhulupirira Uthenga uwu, apita kumadzulo, kenako nakasonkhana kumeneko, ine ndikutanthauza?**

**377. Ndipo kodi** (Tsopano, miniti chabe, izi ndi... kubweretsa...Mphindi chabe. O! Ayi, si choncho, ilo liri ndi “R-e-v.” Ine ndimaganiza...Ndi mutu wa Chivumbulutso, ndipo zimawoneka ngati “M’busa Capps,” ndipo i—i—ine ndinali basi pang’ono—ndinasokonezeka pang’ono ndi zimenezo. N...Ngati inu mungati muwone, izo ndithudi zikuwoneka motero. Mukuona? Izo zinali “M’busa Capps” ndiyeno zinapitirira apa...Ayi, ziri bwino.) **Chivumbulutso mutu 12, ukukamba za Mkwatibwi?**

<sup>11</sup> Ayi! “Tsopano, kodi Mkwatibwi kenako apita kumadzulo, kenako?” Osati momwe ine ndikudziwira izo; Mkwatibwi ndi wakonsekonse, pa dziko lonse lapansi. Tsopano, aliyense amene akumvetsa zimenezo anene, “Ameni!” [Osonkhana ayankha, “Ameni!”—Mkonzi.]

Ziribe kanthu kumene inu muli, kumene inu mukafere, chirichonse chimene chiri, ngati inu mufera mwa Khristu, Mulungu adzakubweretsani inu ndi Iye. Ziribe kanthu ngati inu mwawotchedwa, kudyedwa, kuwonongedwa, mulimonse momwe izo ziriri, Mulungu adzakubweretsani inu ndi Khristu pamene Iye azibwera. Inu simukusowa kuti mukasonkhane

kumadzulo kapena kulikonse. Kulikonse kumene Ambuye akutsogolerani inu . . .

<sup>12</sup> Komabe, ngati inu mukumverera kuti inu mukufuna kuti mupite kumadzulo, ndiroleni ine ndizipangitse izo kumveka bwino kwenikweni basi tsopano, ine ndisanapite. Tsopano, kotero . . . (Kodi iwo akuwujambula uthenga uwu? Iwo akutero? Chabwino.) Inu musandilore ine kuti ndikuuzeni koti mupite. Ngati inu mukumverera kuti mukufuna kuti mubwere uko kummwera, bwerani uko kummwera. Ngati inu mukumverera kuti inu mukufuna kupita kummawa, kumpoto, kumadzulo, kummwera, inu pitani kumene Ambuye akukutsogolerani inu. Aliyense amene akumvetsa zimenezo anene, “Ameni!” [Osonkhana ayankha, “Ameni!”—Mkonzi.]

<sup>13</sup> Ine sikuti ndikuyesera kuti ndimuuze aliyense koti asapite. Ndipo ngati inu mubwera uko ku Tucson, Arizona, kumene ine ndikukhala mongoyembekezera pa nthawi iyi . . . momwe ine ndinakuuzirani inu mmawa uja, ine ndikupukwa kwathu wopanda kwathu koti ndizipitako. Ine ndikukhumba ine ndikadakhala ndi winawake, malo enaake amene ine ndikanamawatcha kwathu kuti ndizipitako. Ngati, usikuuno ngati ine ndikadakhala ndi madola zikwi khumi ndipo ndikanatha kupereka malo pofuna . . . ndi kupereka izo mwaufulu kuti ndipeze kwinakwake kumene ine ndikanatha kumati, “Awa ndi malo amene ine ndikufuna kuti ndiziwatcha kwathu,” ine ndikanati ndipereke izo mwaufulu. Ine ndiribe malo.

M'bale Freeman, ine basi . . . inu mwandidziwa ine kuyambira ndiri mnyamata; i—i—ndine woyendayenda. Musati mudzakhale konse woyendayenda; pezani malo ena amene inu mukuwakonda ndi kukhazikika uko; nkumawadikirira Ambuye Yesu.

<sup>14</sup> Koma ngati inu mukufuna kuti mubwere kumadzulo ku Tucson, Arizona, kumene ine ndikukhala, mwalandiridwa; ine ndikakhala wokondwa kukakhala ndiri nanu. Inu ndi m'bale wanga, mlongo. Ine ndingachite chirichonse mdziko kuti ndikuthandizeni. N—ndipo nonse inu amene mwabwera uko, ine ndikuyesetsa mopambana momwe ine ndikanathera kuti ndikupangeni inu kukhala olandiridwa, ndi kukuwonetsani inu chirichonse chimene ine ndikuchidziwa, ndi kukutengerani konse konse, kuchita chirichonse chimene ine ndingathe kuchita. Ndipo inu ndinu olandiridwa nthawizonse.

<sup>15</sup> Koma ngati inu mukubwera uko pansu pa zikhaldwe izi, kuganiza kuti Mkwatibwi kapena chinachake chidzapita mmwamba kuchokera ku Tucson, Arizona, ndi uko kokha, inu mwalakwitsa. Musati mubwere uko pofuna zimenezo, musati mubwere pofuna zimenezo, chifukwa uko ndi kulakwitsa. Izo si zolondola.

16 Tsopano, Chivumbulutso mutu wa 12...Koma chinthu chimodzi chokha Ambuye akuwululira kwa ine kapena akukhala ngati akuyankhula kwa ine...ine ndangochokera mu masomphenya (inu mukuona?), ndipo ndi zokhala ngati zovuta kuti ndiziletse izo. Mukuona? Koma Iye akuwoneka kuti akuyankhula kwa ine kachiwiri kuti ndinene kachiwiri mochuluka za kupita kumadzulo uku.

17 Tsopano, monga ine ndinanena kale, ine sindiri kunja uko kuti ndingokhala ndiri kumeneko, ine ndiri kumeneko chifukwa ine ndikutsogozedwa kuti ndikakhale ndiri kumeneko. Koma kukakhala kumeneko, kukupanga uko kukhala kwathu, ine ndikuganiza uko nkulakwitsa. Ayi, ine ndikuganiza izo sizikakhala ziri koma basi kanthawi kakafupi chabe mpaka cholinga chimene Mulungu wanditumizira ine kumeneko chidzakhale chitakwaniritsidwa. Ine sindingati ndikuuzeni inu pano chifukwa chimene ine ndikupitira, koma ine sindikanati ndipite pongofuna kuti ndipite.

18 Izo zinafunsidwa mu funso tsiku lina: “Ife tikudziwa chifukwa chimene inu munapitira ku Arizona poyamba, anali Angelo aja amene anakawonekera. Nchifukwa chiyani inu munabwererako nthawi yachiwiri?” Inu mukulikumbukira funso limenelo ndinaliwerenga?

19 Ndi angati amene akukumbukira pamene ine ndinabwerera zitachitika zimenezo ndipo ndinali nditakhala apo pamaso pa Dr. Lee Vayle (ine ndikukhulupirira kuti iye ali mu chipindachi penapake) ndi mkazi wanga? Ndipo ine ndinali kulankhula za Arizona ndi za ife kumakhala kuno, ndipo apo panabwera dzanja pa khoma ndi kuwala ndipo linalemba ndi zilembo, “Bwereranso ku Arizona.” Ndi angati akukumbukira zimenezo? Ndi chifukwa chake ine ndibwerera kumeneko. Ndisakudziwa chifukwa chimene ine ndinabwerera, ndipo pamene ine ndinabwerera kumeneko, ndiye Iye anawulula chifukwa chake ine ndikuyenera kubwererera kumeneko. Ndipo ngati ine nditi ndizinene izo, ndiye Satana azitchinga izo. Koma iye sakuwudziwa mtima wanga. Iye si Mawu, kotero iye sakuwudziwa mtima wanga. Koma ngati ine ndichinena icho, ndiye iye achimva icho. Kotero tsopano, zikumbukirani zimenezo.

20 Tsopano, pamene ine ndinanena tsiku lina, ine ndinakhala ngati ndazipanga izo...Zikukhala ngati mwinamwake inu mukhoza kukhala ndi kukhuzidwa kolakwika; ine ndinati, “Musati mubwere ku Arizona.” Mukuona? Ine sindimatanthauza zimenezo, “Musati mubwere!” Chimene ine ndimatanthauza chinali: Ngati inu mwatsogozedwa kuti mubwere, inu pitirirani nazo chitani izo, ngati inu mwatsogozedwera ku California, Arizona, kulikonse kumene inu muli. Koma ngati inu mukupita kumeneko, mukuti, “M’bale Branham, ine ndikupita kumeneko, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti inu mukupita kukakhala

kumeneke ndi kumakalalikirira Mawu,” ine ndikukhulupirira kuti inu mukulakwitsa pamenepo. Mwaona? Kumene kulalikirira kwanga kuli, ndi komwe kuno ku kachisi uyu; awa ndiwo malowo.

<sup>21</sup> Ine sindikukhala ndi utumiki umodzi mu Arizona. Ndipo ine sindimakhala ku Arizona kupatula basi maora angapo okha pa nthawi. Ine ndiribe. . . Ine ndiri ndi msonkhano wa Amuna Amalonda ikatha Khrisimasi, koyambirira kwa chaka, ku Phoenix. Ndi wokhawo umene ine ndiri nawo; ine ndinalonjeza umenewo, palibe winanso.

<sup>22</sup> Msonkhano wanga wotsatira, momwe ine ndikudziwira, ndi komwe kuno ku 8th ndi Penn Street ku Branham Tabernacle. Ine ndiri ndi maphunziro sate kapena forte amene ine ndikudziwa kuti adzatenga sabata kapena ziwiri pa nthawiyo kuti ndidutse mwa iwo, zimene ine ndiri nazo pa mtima wanga kuti ndizilalikire pano pa Branham Tabernacle, komwe kuno ku Jeffersonville, Indiana.

<sup>23</sup> Ndipo tsopano, ngati inu mukufuna kwenikweni kuti mupite kwinakwake kuti mukakhale ndi Mawu, kumene Uthenga wathu. . . Ndipo Uthenga wathu si wosiyana, ndi Uthenga womwewo umene inu mwaumva moyo wanu wonse, kungoti chinachake chochulukirapo chaululidwira kwa Iwo. Uthenga uwu ndi Uthenga womwewo umene Lutera ankalalikirira, Uthenga womwewo umene Wesile ankalalikirira, Uthenga womwewo umene Achipentekosite ankaulalikirira, kungoti chinachake chawonjezedwa kwa Iwo. Chimene chiri, ndi kuwululidwa kwa Zisindikizo, zimene okonzanso aja anazisiya (mwaona?), zimene zadziwitsidwa mu tsiku lino sizikanati zidziwitsidwe apo. Uthenga wa Chipentekosite sukanati udziwidwe mu masiku a Lutera ndi Wesile; izo zinkayenera kudikirira mpakana m’badwo wa Chipentekosite. Koma m’badwo wa Chipentekosite si china koma m’badwo wopitirira wa Chilutera. Monga ngati chimanga chikamakhwima kapena china chirichonse, chomwecho mpingo watero.

<sup>24</sup> Ngati ine ndikanati ndilalikire usikuuno, ine ndikanati ndilalikire pa phunziro, ndasonyeza apa mu Baibulo, “*Mpesa umene unasamutsidwa kuchokera ku Igupto kupita mu Palestina.*” Ndi angati a inu amene munayamba mwadziwa kuti Mulungu anali atanena kuti Israeli anali mpesa Wake? Ndiye ine nkulozera mmbuyo kuchokera apo kwa Yesu kukhala ali Mpesa. Ndipo Mpingo tsopano wasamutsidwira ku dziko, sunakhazikidwe mu dothi, koma wakhazikitsidwa mwa Khristu, pamene ukuyenera kuti ubale chipatso. Mukuwona? Ndipo umenewo ukanati ukhale uthenga wanga wa usikuuno ngati ine ndikanati ndilalikire. Koma ine ndinaganiza kuti ine kulibwino nditenge mafunso awa, kotero ine ndinangoulumpha uwo. Ine ndidzautenga uwo mwinamwake pamene ine ndidzabweranso.

<sup>25</sup> Chivumbulutso mutu 12 siwokamba za Mkwatibwi. Chivumbulutso mutu 12 (ine sindinaziyang'ane izo umo koma ine ndikuzidziwa izo), ndi mkazi ataima mu dzuwa ali ndi mwezi pansi pa mapazi ake. Mwezi umaimira lamulo; mkazi amaimira Israeli, mpingo; ndipo nyenyezi khumi ndi ziwiri pa mphumi pake anali atumwi khumi ndi awiri aja, mibadwo khumi ndi iwiri, ndi zina zotero, imene yangotha kumene. Mukuona? Ndipo dzuwa linali pa mutu pake. Chimene inu mukuwona, mwezi ndi mthunzi wa dzuwa, chimene lamulo linali mthunzi wa zinthu zabwino zakuti zibwera. Ndipo mkazi ameneyo ndi Israeli, osati Mkwatibwi.

Tsopano ine sinditaya nthawi yambiri, chifukwa ine ndiyenera kuti ndiwafikitse iwo pakutha.

**378. Aroma 7:14-18, “Ife tikudziwa kuti lamulo liri lauzimu: koma ine ndine wachithupi thupi, wogulitsidwa pansi pa tchimo. Pakuti icho chimene ine ndikanati ndizichita—osati: pakuti chimene ine ndimafuna, icho ine sindimachichita; koma chimene ine ndimadana nacho, chimenecho ine ndimachichita. Ngati ndiye ine ndimachita icho chimene ine sindimafuna kuchichita, ine (n-d-i-t-h-a-. . .) k—kwa lamulo, kuvomereza kwa lamulo, kuti ilo ndi labwino. Tsopano ndiye, si inenso amene ndimachita zimenezo, koma tchimo limene likukhala mwa ine.” Izi ine sindikutha kuzimvetsa.**

<sup>26</sup> Chabwino, iwo analilemba apo Lembalo; ameneyo ndi Paulo akuyankhula kwa Aroma. Tsopano iye akuti. . . Ndiroleni ine ndingokhala ngati ndazipukuta izo kuti inu mukhoze kuziwona. Iye anati, “Mwa ine muli anthu awiri: zolondola, mmodzi amafuna kuti ine ndizizichita; zolakwika, winayo amafuna kuti ine ndizizichita. Ndipo nthawizonse ine ndikayamba kuchita zolondola, ndiye zolakwika zimanditchinga ine.”

<sup>27</sup> Ndi angati mwa anthu inu a pa zoyankhulana madzulo awa munakumana nacho chinthu chomwecho, ndi mmawa uja (mwaona?), chinthu chomwecho? Ine ndinayankhula pa icho mmawa uja, mosakhazikika.

<sup>28</sup> Inu ndinu munthu wakunja amene ali kulamuliridwa ndi mphamvu zisanu ndi imodzi; inu ndinu munthu wamkati wolamuliridwa ndi mphamvu imodzi imene ili chikhulupiriro. Ndipo chikhulupiriro ichi chimatsutsana ndi mphamvu zonse zisanu ndi imodzizo ngati mphamvu zisanu ndi imodziyo sizikugwirizana ndi chikhulupiriro. Koma imodzi ndi yosiyana kwa inayo. Tsopano, bola ngati mphamvu zisanu ndi imodzizo zikugwirizana ndi chikhulupiriro, nzodabwitsa; koma pamene mphamvu zisanu ndi imodzi zikutsutsana ndi chikhulupiriro, ndiye muzizisiya mphamvu zisanu ndi imodzizo zokha.

<sup>29</sup> Tsopano, mwa chitsanzo apa, Yesu anapanga neno, lonjezo. Munthu wamkatiyo akati izo ndi zoono; munthu wakunjayo

amalingalira kuti izo sizingakhale zoonza kwa iwe, ndiye usamusamale munthu wakunjayo ndi kumuvomereza munthu wamkatiyo. Tsopano, icho ndi chinthu chofanana chimene Paulo akuchikamba. Iye anagulitsidwa pansu pa lamulo kwa tchimo lachithupithupi. Aliyense wa ife ali chimodzimodzi. Ndicho chifukwa ife tiri. . . tiri nao mavuto amene ife timachita, okwatira kanai kapena kasanu, ndi *izi*, ndi *izo*, ndi. . . mitundu yonse ya tchimo, ndi zigololo, ndi chinthu china chirichonse zotsatira mmiyoyo yathu, ndi chifukwa cha zinthu zimenezo. Ife ndi achithupithupi, ndipo gawo limenelo liyenera kuwonongeka; komano, mkatimu, ife ndife munthu wauzimu, solo mkatimu, ndipo chimenecho ndi chikhulupiriro mu Mawu a Mulungu; ndiye ife timalibweretsa thupi lathu lakunjali pansu pa kumvera ku Mawu mwa chikhulupiriro, pa kuvomereza zimene Mulungu ananena.

<sup>30</sup> Ine ndingathe bwanji kutenga chisoso ndi kupanga mbewu ya tirigu kuchokera mwa icho? Izo ndi zosatheka kuti ine ndichite zimenezo? Njira yokha imene izo zingakhaliye ziri chifukwa cha mkati mwa chisoso chimenecho mwasamutsidwa kuchokera ku chisoso cha tirigu. . . chisoso kukakhala nyongolosi yotchedwa “moyo wa tirigu.” Ndiye inu mukakwirira chisoso chimenecho, ndipo icho chibala njere ya tirigu (uko nkulondola. Mukuona?), chifukwa pakhala pali moyo wa tirigu umene waikidwa mu chisosocho. Ndipo moyo wa chisoso wachotsedwa umo; koma chikhalidwe cha chisoso chikanali chobaya (mukuona?), ndipo icho chikhala chiri mpakana moyo watsopano uwu ukhale utawumbidwa kwathunthu kuchokera mu nthaka ndi kuwukitsidwa apo kachiwiri. Pamene icho chizitulukira apo, ndiye icho sichilinso chisoso, koma tiri—koma tirigu. Koma pamene icho chikadali kuno pa dziko lapansi ndipo. . . mu. . . kuchokera pa dziko lapansi. . . Ndipo chisoso, chikanali chobaya, koma icho chiri ndi chikhalidwe mkati mwakemo cha tirigu.

<sup>31</sup> Ndipo utali wonse pamene inu muli mu moyo uno, inu muzikhala muli obaya ndi kumakhala ndi chikhalidwe cha chithupithupi chimene chizikuvutitsani inu utali wonse pamene inu muli amoyo; koma mkati mwa inu, inu ndinu obadwa kachiwiri. Ndipo pamene inu mudzaukitsidwa, inu muli mu kufanana ndi Khristu ndipo machimo onse achoka mwa inu. Mukuona? I—icho ndiye chinthucho.

<sup>32</sup> Mundirole ine ndinene ichi? Izo zikumveka ngati nthabwala. Mmwenye. . . Iwo ndi anthu oseketsa kwambiri. Ndipo ine. . . Iwo si oseketsa; iwo ndi osamvetsetseka kwa ife; koma iwo amawoneka kuti ali bwino bwino kwa iwoeni. Ndipo ngati inu mufika powadziwa iwo, iwo ndi abwino bwino. Mmwenye anafunsiwa nthawi ina pamene iye anapulumutsidwa. . .

<sup>33</sup> Ine ndikukumbukira mmodzi mu Phoenix, Arizona. Billy anali kupita kuti akapereke makadi apemphero. Ndipo iye



amangoima pamenepo ndi kumapereka makadi apempherowo. Ndipo anthu amenewo ankatha kuthamangira apo ndi kukatenga makadi apemphero. . . Pamene—anthu abwino bwino kwenikweni anali ndi kupweteka kwa mutu, kupweteka kwa dzino, kapena chinachake chitavuta ndi zala zazikulu zakuphazi zawo, iwo amala—iwo amalandira makadi apemphero, M'bale Ruddell. Ndipo p—pamene iwo anatero, ndiye mu mzere wapemphero, chinthu chokha chimene ine ndinali nacho, winawake ali ndi kupweteka kwa mutu, winawake anali ndi chinachake chitavuta ndi chala chachikulu chakuphazi chake, ndi chinachake chonga choncho. Ndipo apo panali anthu atakhala pamenepo akufa ndi khansara ndi zinthu amene sanafike pa mnzere wapemphero. Ine ndinati, “Billy, pita uko pansipo ndi kukawafunsa anthu awo chomwe chiri vuto ndi iwo. Ndipo ngati iwo alibe khansara, kapena matenda ena owopsya, kapena chinachake chimene chiti chiwaphe iwo, usati uwapatse iwo makadi apempherowo. Atengere anthu amenewo pamwamba apo mu mzere wapemphero a. . . amene atsala pang'ono kufa ngati iwo sathandizidwa kuchokera kwa Ambuye. Asiye enawo kuti angodikira. Asiye iwo abwere mu mzere wofulumira kapena chinachake. Koma alole anthu awo amene atsala pang'ono kufa. . .” Ine ndinati, “Ziwafunsa iwo.”

Iye anati, “Chabwino, inu munati, ‘ine ndizingosakaniza makadi ndi kuwapereka iwo kwa iwo. Ndi chimene ine ndinali kuchita.”

Ine ndinati, “Koma iwe ukuwapangitsa anthu awo kumathamangira kutsogolo kwa iwo, ndipo awo akulandira. . . Osauka olumala awo ndi zinthu sakutha kuwalandira iwo.”

“Chabwino, ine ndikachita izo.”

Iye akupita uko; uko kunali Mmwenye wokalamba (ndipo iwo ndi osamvetsetseka kwambiri) iye samalola kukhala pansu mu mpando. Iwo anamupatsa iye mpando, koma iye anangokhala pansu pabwalo mu hemayo. Iye anali atavala chipewa; iye samalola kuti achivule icho; anali ndi nthenga itasomekedwa kumbuyo kwa icho, atangokhala pamenepo.

Billy anayenda napita kwa iye, ndipo iye anadutsa pamenepo, ndipo iye anati, “Inu mukufuna khadi lapemphero?”

“Nhuu.”

Iye anati, “Vuto lanu ndi chiani, Mfumu.”

Iye anati, “Ine kudwala!”

Iye anati, “Koma vuto lanu ndi chiani inu?”

Iye anati, “Ine kudwala!”

Iye anati, “Koma ine ndikufuna kuti ndidziwe lomwe liri vuto lanu!”

Iye anati, “Ine kudwala!”

<sup>34</sup> Ndi zokhazo zimene iye akanapeza kuchokera mwa iye, anati, “Chabwino, ine ndibwerera pakapita kanthawi.” Kotero Billy anapitirira pamenepo kumawafunsa anthuwo. Mmwenye wokalambayo anapitiriza kumawayang’ana makadi apemphero awo akuchepera chepera. Nthawi iliyonse iye amawatulutsa iwo mthumba mwake, iwo anali kucheperapo pang’ono kwambiri. Kotero patapita kanthawi, Mmwenye wokalambayo anaimirira, ndipo anayenda, ndi kudzamukodola Billy pansana kuti amukumbutse iye kuti nayenso anali mu izi. Iye anati—iye anati, “Mfumu, vuto lanu ndi chiani inu?”

Iye anati, “Ine kudwala!”

Iye anati, “Chabwino, Mfumu, inu muyenera kuti mudiuze ine. Adadi anati ine ndisapereke makadi awa kwa anthu amene anga. . . amene angokhala ndi, monga kupweteka kwa mmimba, ndi kupweteka kwa mitu, ndi zinthu. ‘Ndipereke iwo kwa anthu amene akudwala zenizeni.’” Anati, “Inu mukudwala motani, Mfumu?”

Iye anati, “Ine kudwala.” Iye anamukhazika iye pansa kachiwiri ndipo iye asana. . . makadi ake anali kwenikweni pafupi kutha. Maminitsi angapo. . . Iye anapitiriza kuwayang’anitsitsa makadi amenewo. Iye anabwerera ndi kudzamukodola iye aponso. Iye anafunyulula dzanja lake. Billy anaika khadi pa dzanja lake, anati, “Mfumu, pitani mukalembe pamenepo, ‘Ine kudwala.’”

<sup>35</sup> Iye anafika mu mzere wapemphero, ndipo ine ndinali kumupempherera iye, ndipo ine ndinati, “Kodi inu mukukhulupirira, Mfumu?”

Iye anati, “Uko kulondola.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu?”

Iye anati, “Uko kulondola.”

Ine ndinati, “Inu mukakhala mnyamata wabwino?”

Iye anati, “Uko kulondola.”

Ine ndinakomana naye iye pafupi sabata kenako. M’bale Fred Sothmann ine ndikukhulupirira anali kumeneko. Panali pamene i. . . ndi pamene msonkhano wa mu hema unali kupitirira. Uko kunali ku Phoenix. Ndipo ine ndinakumana naye iye kanthawi pang’ono motsatira mu sabata; ine ndinati, “Kodi inu mukupeza bwino, Mfumu?”

Iye anati, “Uko kulondola.” Ndinadzapeza kuti, ine ndinayankhula mwa. . . Kodi dzina la mmishonare uja uko ndi ndani, bambo wokalamba uja ali ndi ndevu za pamphuno zoyera uja, kumtunda uko kwa Apache? Ine ndikulephera kuganizira dzina lake. O, iye ndi munthu wabwino wachikulire. Mkazi wake anachiritsidwa ku khansa, inu mukudziwa. Iye anati, “M’bale Branham, izo ndi zokha zimene iye angathe kunena.”

Anati, “Ine ndinamuphonzitsa iye kuti aziti, ‘Ine kudwala.’ Ndi chinthu chokha chimene iye angathe kuchinena, ‘Uko kulondola.’” Kotero n—izo ndi pafupi zonse, inu mukuona. “Uko kulondola. Inde kudwala!”

<sup>36</sup> Winawake anandiuza ine kuti iye anali naye, wina, nthawi ina, anali atatembenezidwa, analandira Mzimu Woyera, ndipo iye ananena kwa iye, “Zikuyenda bwanji kwa inu?”

Ndipo iye anati, “Bwino kwambiri ndi moyipa kwambiri.”

Iye anati, “Chabwino, inu mukutanthauza chiani moipa kwambiri ndi bwino kwambiri?”

Iye anati, “Chabwino, kuyambira pamene ine ndinalandira Mzimu Woyera,” iye anati, “mwakhala muli agalu awiri mkati mwanga, ndipo mmodzi wa iwo galu wakuda ndipo mmodzi wa iwo galu woyera.” Ndipo anati, “Iwo amakangana nthawi zonse.” Anati, “Iwo amakuwa ndi kumamenyana wina ndi mzake.” Ndipo anati, “Galu woyera amafuna kuti ine ndizichita zabwino; galu wakuda amafuna kuti ine ndizichita zoipa.”

Anati, “Chabwino, Mfumu, ndi uti mwa iwo amene amawina ndewuyo?”

<sup>37</sup> Anati, “Zimenezo zimatengera uyo amene Mfumu wamudyetsa kwambiri.” Kotero ine ndikuganiza kuti ilo ndi yankho labwino apa. Mukuona? Izo zimagotengera nkondo ya mthupi imene ili mwa inu; izo zimatengera amene inu mumamudyetsa, chikhalidwe chimene inu mumachidyetsa, chikhalidwe chachithupi chotsatira zinthu za mdziko, kapena chikhalidwe chauzimu chotsatira zinthu za Mulungu. Izo zimachititsa zimenezo.

**379. Kodi mwana wa Mulungu aliyense angathe kudzozedwa kwambiri mpakana iye angathe kumachita zozizwitsa, zizindikiro, ndi zodabwitsa, kapena kodi izi ndi basi... kodi izi ziri pa kulondolera kwa Mzimu Woyera?**

<sup>38</sup> Inde, izo ziri pa kulondolera kwa Mzimu Woyera. Ngati iwe uli mwana wamwamuna wa Mulungu, kapena mwana wamkazi wa Mulungu, chirichonse chimene iwe uli, pamene iwe walandira Mzimu Woyera, ndiye Mzimu Woyera umakutsogolera iwe kuti uzichita zinthu.

<sup>39</sup> Ine ndiribe nthawi. Ine ndikungokhumba ine ndikanati ndikuuzeni inu nkhani zazing’ono. Nthawi iliyonse ine ndikaganiza za izo, ine ndimangodutsa pa izo. Koma ine ndikuganiza iyi igwira kwa miniti chabe.

<sup>40</sup> Kunali uko ku Meridian, Mississippi. Ambiri a inu anthu aumodzi, M’bale Bigby anali akuchititsa...anali akuthandizira misonkhano yanga, iye ndi m’bale waumodzi. Ndipo usiku umodzi mu msonkhano, Billy Paul anali atapita ku bwalolo ndipo anali atapereka makadi apemphero. O, inali ikukhuthukira pansu mvula. Ndipo anthu anali ataima

panja ndi maambulera ndi zinthu. Ndipo Billy anapereka makadi apemphero, ndipo panali. . . Ndiyeno iye anabwera kuti adzanditenge ine. Ndipo pamene anali. . . pamene iye anali kubwera kuti adzanditenge ine, apo panali dona wamng'ono amene anakhala pansu kutsogolo, ndipo apo panali dona wina akuyenda ali ndi mwana wamng'ono, akuyesera kuti amutonholetse iye. Ndipo dona wamng'ono uyu anakhala pamenepo atavala diresi laling'ono la guta, chirichonse chimene iyo inali, anali mayi nayenso. Ndipo iye anamuwona donayo, ndipo Mzimu Woyera unayankhula kwa mkaziyo, chinachake pa mtima wake, “Pita ukamupempherere mwana ameneyo.”

<sup>41</sup> “Chabwino,” iye anati, “nthawi ina iye akamadutsa, ine ndipita ndikamupempherere iye.” Ndipo pamene iye anadutsa kachiwiri, donayo anali atagwirizira khadi la pemphero. “O,” ine anati, “I—sindingati ndimupempherere mwana ameneyo.” Anati, “M’bale Branham amupempherera mwana ameneyo usikuuno. Ndipo ndine yani kuti ndimupempherere mwanayo ngati M’bale Branham ati amupempherere iye?” Tsopano, uku kunali kulemekeza, ndipo zimenezo zinali zabwino, koma zimenezo nthawizonse sizingakhale ziri chifuniro cha Mulungu. Nthawizina izo zimakhala mosiyana.

Mzimu Woyera unapitiriza kumuuzza iye, “Pita ukamupempherere mwana ameneyo.”

Potsiriza iye anaganiza, “Mzimayi ameneyo andikana ine mochititsa manyazi. Podziwa kuti iye ali ndi khadi lapemphero, iye sangafune kuti ine ndimupempherere mwana ameneyo. Iye anamubweretsa mwana ameneyo kuno, osati kuti ine ndidzamupempherere iye, koma kuti M’bale Branham amupempherere iye.”

Kotero Mzimu Woyera unapitiriza kunena, “Pita ukamupemphere mwana ameneyo.”

Potsiriza iye anati, “Chabwino, kuti ndidzimasule ndekha ine ndingoti. . . Ine ndimupatsa iye mpando wanga.” Kotero iye anati, “Wokondedwa (mayi mmodzi wamng'onoyo kulankhula kwa winayo), kodi i—inu mungafune. . . inu muli ndi mwana uyo. . .” Anati, “Kodi inu mungabwere, mudzakhale pansu apa, tengani mpando wangawu?”

Iye anati, “O, Wokondedwa, ine sindikufuna kuti nditenge mpando wanu.” Anati, “Ine ndikuyesera kuti ndimutonhoze mwanayu.”

Anati, “Koma inu mukuwoneka otopa kwambiri ndi ofooka.”

Iye anati, “Ine ndiri.”

Iye anati, “Chabwino, khalani pansu apa ndi kutenga mpando wanga.” Ndipo iye anati, “Ine ndikuwona kuti inu muli

ndi khadi la pemphero. Mwinamwake ndinu. . . M'bale Branham akuti amupempherere mwana wanuyo?"

Iye anati, "Ife tikuyembekezera kuti nambala iyi iyitanidwa."

Ndipo iye anati, "Chabwino, ine ndikuteronso." Iye anati, "Mlongo kodi inu ndinu Mkhristu?"

Nati, "O, inde!"

Iye anati, "Ine ndine Mkhristu nanenso." Ndipo anati, "Chiyambireni pamene ine ndakhala ndiri pano, Mzimu wa Ambuye wakhala ukundiuza ine, 'Mupempherere mwana ameneyo.' Kodi inu mungandipatse ine chilolezo? Ine ndikudziwa M'bale Branham amupempherera mwana ameneyo ngati ataitanidwe. Ndipo inu mukhale mutagwirizira khadi lanulo, iye ayitenga iyo." Anati, "Koma ngati ine ndingaike manja anga pa mwanayu, ndi kungopereka pemphero laling'ono kuti ndidzipangitse ndekha kumverera bwinoko, ndi kuchoka ku chimene chikundiitana ine, kodi i—kodi izo zingakukhumudwitseni inu?"

<sup>42</sup> Iye anati, "Motani, ayi ndithu, Wokonededwa. Mupempherereni mwanayu." Ndipo iye anali mwana wamng'ono wabuluu, ndipo kotero—dona wamng'onoyo anamupempherera iye. Iye anamupatsa donayu mpando wake, ndipo iye anakwera mmwamba kupita mu chithandala chachitatu ndipo anali ataimirira mmenemo. M'bale wina Wachikhristu pamwamba apo, njonda mokwanira anaimirira kuti amupatse dona uyu pokhala, kotero iye anakhala pansu.

<sup>43</sup> Pafupi theka la ora kenako, ine ndinabwera mu msonkhanowo, ndinayankhula kwa maminitsi pang'ono, ndinaitana makadi apemphero; ndipo mkazi uyu anali wachitatu kapena wachinai mu mzere ndi mwana ameneyo. Ndipo iye anakhala pamenepo, ndipo iye anati, "O, zikomo inu, Ambuye. Tsopano, ine ndinamumvera chisoni mayi wamng'ono ameneyo, ine ndikukhulupirira kuti mwanayo akhala bwino tsopano, chifukwa M'bale Branham. . . Ndi wachitatu kapena wachinai basi, iye afika kwa ameneyo." Anati, "Zikomo inu, Ambuye," mayi wamng'onoyo atakhala pamenepo, akumumvera chisoni mwana ameneyo. Chabwino.

<sup>44</sup> Ndiye pamene ine ndinabwera apo, ndinayamba kumupempherera mwanayo, pamene donayo anabwera apo, nditi, ine ndinayang'ana pa iye ndipo ndinati, "Tsopano, mwana wanu ndi mwana wabuluu. Inu mwamubweretsa iye kuno kuti adzapemphereredwe. Ndipo tsopano, dzina lanu ndi Akazi a *Wakuti-ndi-wakuti*, ndipo inu mwachokera ku malo *Akuti-ndi-akuti*; koma mwanayu wachiritsidwa kale. Panali mkazi amene anali ndi kulemedwa pa mtima wake dzina lake ndi Akazi *Akuti-ndi-akuti*, amene wakhala pamwamba apa mu thandala (woyambirira kumapeto kwa mzere wachinai mu

thandala lachitatu), anapemphera pemphero lachikhulupiriro kwa mwanayo; ndipo mwanayu wachiritsidwa kale.” Iye anali ngati angogwa kuchokera mu mpando wake. Mukuona?

<sup>45</sup> Tsopano, nanga bwanji ngati iye akanati asachite zimenezo? Inu mukuwona zimene ine ndikutanthauza? Tsopano, mayi ameneyo akadakhala ndi chisoni chochulukirapo kwa mwana ameneyo, mayi kwa mwana kuposa momwe ine ndikanachitira kwa mwanayo. Mwawona? Ndipo mayiyo pokhala . . . Mukuona?

<sup>46</sup> “Kodi ife tonse tingathe kumachita zozizwitsa?” Inde. Pamene iwe watsogozedwa ndi Mzimu Woyera kuti uchite zozizwitsa, pita uzikachita izo, chifukwa ndi kutsogoza kwa Mzimu Woyera.

<sup>47</sup> Tsopano, ngati mkazi ameneyo akanati asachite zimene Mulungu anamuuzwa iye, mwinamwake pakanakhala kudzudzula mwa Mzimu kwa iye (inu mukuona?), ndipo iye akanakhala asanamumvere Mulungu. Nthawizonse, ngati inu muli Mkristu ndipo chinachake chikukukakamazani inu kuti muchite chinachake, pitani kachiteni icho. Pitani mukachite icho; musati mukaikire icho; pitani mukachite icho.

“Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi funso. Kodi . . .” Apa pali lina la iwo, kapena ine ndinalitenga ilo molakwitsa . . . Eya, i . . . ilo ndi lina la mmawa uno. “Mkazi kuvala zovala zogonera, kodi izo ndi zovala zachimuna?” Ilo liyenera kuti linasakanizika apa mu ena awa.

“M’bale Branham, kodi Mulungu anali akuchita chinthu . . . kodi Mulungu . . . kodi ine ndinali ndikuchita chinthu chimene chinachitika pamene tepi . . .” O, inde, ife tinali nalo ilo mmawa uja. Ine ndiyenera kuti ndinawasakaniza ena a amenewo. Ine ndimayenera kuti ndiwang’ambe iwo, koma ine ndikungodana nazo kuti ndichite zimenezo.

**380. M’bale Branham, ndi ndani amene ati adzalidzazitse dziko kunja kwa Mzinda Wakumwamba?**

**381. Tafotokozani za m’ngelo wa munthu aliyense amene amakhala nawo iwo kuchokera pakubadwa mpakana pa imfa. Funso labwino kwambiri.**

<sup>48</sup> Ine ndikudana nazo kungowadutsa awa apa; awa ndi mafunso abwino. Ndipo ine ndikufuna a—ana anga kuti azidziwa zinthu zimenezi. Mukuona? “Tsopano, ndani amene ati adzalidzazitse dzikoli kunja kwa Mzinda?” Kunja, awo adzakhala ali owomboledwa amene ati adzalidzazitse dziko lapansi, kunja kwa Mzinda, koma iwo sadzakhala ali Mkwatibwi wosankhidwa ndi woitanidwa. Mkwatibwi azidzakhala mkati mwa Ufumu limodzi ndi Mfumu. Kunjako kuzidzakhala mafumu a dziko lapansi amene azidzagwira ntchito ndi kumabweretsa zovutikira zawo, kumabweretsa zawo . . . osati zovutikira zawo, koma azidzabweretsa zipatso zawo mu

Mzindawo. Ndipo zitseko sizimadzakhala zitatsekedwa mu usiku.

49 Tsopano, pa . . . Tsopano, Kuwala uku pamwamba pa phiri sikumadzawalitsa dziko lonselo, Iko kuzidzangomawalitsa Mzindawo. Koma Iko kuzidzakhoza kumawonedwa pa mtunda wa zikwi za mailosi mwinamwake; koma Iko sikumadzawalira dziko lapansi, chifukwa Baibulo linati, mu Dziko Latsopano, kuti kuchokera ku Sabata limodzi kupita ku lina ndi kuchokera ku lim—kuchoka ku mwezi umodzi kupita kwa winawo (inu mukuwona?) anthu azidzabwera uko pamaso pa Ambuye kufika ku Zion. . . kufika ku Mzinda kuti akapembedze.

50 Ndipo tsopano, iwo azidzakhala ali kunja kwa Mzinda, osati Mkwatibwi, koma anthu amene akubwerapo mu chiukitsiro chachiwiri amene ati adzakhale olima a nthaka, monga momwe Adamu analiri, ndi ena otero, ndi osamalira a mundawo. Koma Mfumu ndi Mfumukazi azidzatsalira mu Mzindawo.

51 “Tafotokozani za mngelo wa munthu aliyense amene amakhala nawo kuchokera pakubadwa.” Tsopano, ngati inu mungazindikire. . . Tsopano, izi ndi zakuya kwenikweni. Tsopano, ine sindina. . . ine ndinangozitola izo apo. Tsopano, g. . . Gawo lina lataipidwa ndipo linalo liri mu pensulo—kapena peni.

52 Tsopano, pali Mngelo, koma Mngelo uyu wa Ambuye amene amazinga pa iwo amene amawaopa awo . . . amene amamuwopa Iye. Mukuona? Tsopano, awo sanalonjezedwe kuti ochimwa ali ndi Angelo, ndi owomboledwa okha amene ali ndi Angelo. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Angelo a Ambuye amazinga pa iwo amene amamuwopa Iye.

53 Tsopano, Angelo ndiwo amithenga. Ine ndikufuna inu kuti muzidziwe Izo ndi zangwiro kwambiri, ndipo izo zitsimikizira kukonzedweratu kwa inu. Mukuona?

54 Tsopano, pamene mwana wakhanda ali kupangidwa pansu pa mtima wa make. . . Ndipo ana aang’ono inu amene mukuzimvetsa zinthu izi, onani, Ambuye anakuperekani inu kwa amayi. Ndipo iwo anakunyamulani inu pansu pa mtima wawo, chifukwa inu ndi apafupi kwa mtima wawo. Ndiyeno, tsiku lina Ambuye anatsika ndipo anakuwombolani inu kuchokera ku mtima wa amayi, kukuchotsani inu ku mtima wawo, koma inu nthawizonse muzikhala muli mu mtima wawo.

55 Tsopano, pamene thupi laling’ono ili liri nkuumbidwa, thupi laling’ono lachibadwa likakhala likuumbidwa mwa amayi, pali thupi lauzimu la padziko lokonzekera kuti lililandire thupi lachibadwa ili mwamsanga pamene ilo labadwa. Tsopano, mwana amabadwa ndi akatumba amoyo, mtima ukugunda, koma wopanda mpweya wa moyo mwa iye. Akatumba ake akututuma. . . Mukuona? Ndiye, onani, ngati pakhala pali chinachake chosiyana kwa zimenezo, ngati pakanati pasakhale

mzimu umene ukanayenera kudzalowa mu ilo kenako, ndiye mpweya wathu ukanatichokera ife, ndipo ife sitikanati tipume kenanso ndi kukhalabe tiri amoyo. Koma pamene thupi ili sililandira mpweya kuchokera ku...kapena mpweya (kulowetsedwa ndi kutulutsidwa mu mapapo athu), ndiye ife ndi akufa.

<sup>56</sup> Tsopano, koma pamene mayi...Mwana wamng'ono agwetsedwa ku dziko lapansi kuchokera ku mtima wa amayi ake. "Agwetsedwa," inu mukumvetsa zimene ine ndikunena, momwe ine ndiri...chifukwa chomwe ine ndikunenera izi mwanjira iyi. Pamene mwana wamng'onoyo agwetsedwa, chimachitika ndi chiani? Mwamsanga pamene iye atulukira apo, ngati iye sayamba kulira, adokotala, anamwino, kapena aliyenseyo, amamunya iye [M'bale Branham awomba manja ake—Mkonzi.], kumuwongola iye. Akuyenera kukhala ndi kudzidzimuka, ndipo chimachitika ndi chiani?

<sup>57</sup> Zindikirani, mayi, iye akhoza kukhala wankharwe kwambiri ndi wankhanza, koma basi mwana ameneyo asanabadwe, pamakhala pali chifundo chinachake chimene chimakhazikika umo. Kodi inu munayamba mwamuzindikira mayi pamene iye akukonzekera kuti akhale mayi? Pamakhala chinachake chokoma pa iye; iye nthawizonse amatengapo kukoma kumeneko. Ndi chifukwa chakuti mngelo wamng'ono uyo, mzimu waung'ono, mthenga wamng'ono kwa kachisi wamng'ono uyu wakonzeka kuti abwere apo kulowa mu dziko. Ndiyeno, pamene mngelo wamng'ono uyu abwera mu thupilo (uyo ndi mngelo wamng'ono wa padziko lapansi, mzimu umene unadzedwa ndi Mulungu kuti udzalitenge thupi ili), ndiye mwana ameneyo ayenera kukhala nako kusankha. Iye amapanga kusankha kwake. Ndiye pamene izi zichitika, ndiye, inu mukuwona, Mngelo wa Ambuye tsopano amabwera mkati umu, limene liri thupi lauzimu, Lamuyaya ilo.

<sup>58</sup> Uwu ndi mzimu wakufa mu thupi lakufa; koma tsopano, inu simungati muzikhala mu matupi awiri pa nthawi imodzi, koma pakhoza kukhala zikhalidwe ziwiri mwa inu pa nthawi imodzi. Tsopano, chikhalidwe cha Mzimu wa Ambuye... Pamene inu mwabadwa kachiwiri, inu simumabadwa mwathupi, monga mwanayo anachitira; koma chimene chachitika, kubadwa kwauzimu kwabwera mkati mwa inu. Ndipo pamene kubadwa kwauzimu uku kukukula mu mtima mwanu, kwa Mulungu, pamakhala pali thupi logwirika kapena thupi lakumwamba limene likukula kuti liulandire mzimu umenewo. Ndipo pamene moyowo uchoka mu thupi ili, iwo umapita kwa thupi limenelo. Basi monga pamene thupi limaperekedwa kwa dziko lapansi, mzimu umabwera mmenemo, ndipo pamene mzimuwo utuluka mu thupilo, pali thupi likudikira. "Pakuti ife tikudziwa kuti pambuyo pake msasa wapansi uwu udzakhala ukusungunuka,



ife tiri nawo kale wina ukuyembekezera.” Mukuona? Ndi zimenezo, thupi lauzimu la anthu.

**M’bale Branham . . .**

Tsopano, awa akhoza kukhala . . . Pali gulu la iwo pano, akuwoneka ngati teni kapena fifitini. Iwo onse alembedwa pa pepala, pepala la mtundu wofanana, kulemba kwa taipi, ndi zina zotero. Ine ndiyesera kuti ndifike kwa iwo mofulumira momwe zingathekere. Ife tikhoze kutuluka mu . . . mwamsanga momwe tingathere.

**382. Wokonedwa m’bale, kodi Yesu sakadavomereza kupembedzedwa mu Chivumbulutso ndi Yohane pamene iye anagwa kuti . . . Chifukwa chiyani Yesu sanalandire kupembedzedwa mu Chivumbulutso kopangidwa ndi Yohane pamene Iye—pamene Iye anavomereza kupembedzedwa pamaso pa iye? Chifukwa chiani Yesu sanalandire kupembedzedwa pamene Yohane ankafuna kuti amupembedze Iye?**

<sup>59</sup> Wokonedwa m’bale wanga kapena mlongo, aliyense yemwe ali, uyo sanali Yesu amene anakana kulandira kupembedzedwa. Mu Chivumbulutso 22:8, inu muwerenga kuti anali mneneri, mngelo, amene sanafune kulandira kupembedzedwa. Pamene Yohane anagwera pansi kuti amupembedze mngelo amene anali atamuwonetsa iye zinthu izi, iye anati “Ona kuti iwe usachite izo, pakuti ine ndine wa abale ako omwe. Ine ndine mmodzi wa aneneri.” Mukuona, mukuona? “Ine ndine m’bale mzako, wantchito mzako, mmodzi wa aneneri; zipereka mapembedzo kwa Mulungu.” Uyo sanali Yesu amene sakanati alandire izo, uyo anali mneneri amene sakanati alandire izo.

**383. Wokonedwa M’bale Branham, kusiyana ndi chiyani pamene Yesu anapumira pa ophunzira ndipo anati, “Landirani inu Mzimu Woyera,” ndi pamene i—pamene iwo anachita kupita ku chipinda chapamwamba kuti akadikirire?**

<sup>60</sup> Ilo linali lonjezo limene Iye anawapatsa iwo, anapumira pa iwo lonjezo Lake, anati, “Landirani inu Mzimu Woyera.” Ilo linali lonjezo. Iwo anapita ku chipinda chapamwamba kuti akadikirire lonjezolo kuti likakwaniritsidwe.

<sup>61</sup> Chinthu chofanana chimakhala pamene ife tiika manja pa inu kuti muchiritsidwe, ndiye inu mumapitirira kumakachita ntchito zanu mukudikirira lonjezolo kuti likakwaniritsidwe.

**384. M’bale Branham, kodi Yesu anasinththa maonekedwe ake athupi kangapo pamene anali kuwonekera kwa ophunzira pambuyo pa chiukitsiro Chake?**

<sup>62</sup> “Kodi Iye anasinththa maonekedwe Ake a thupi?” I—ine sindikanati ndidziwe, chifukwa ine ndikuganiza chomwe icho chinali, Iye sanasinththe maonekedwe Ake pamenepo. Chinthu

chimene Iye ankachita, Iye ankawalepheretsa kuwona kwawo kapena kumudziwa Iye.

<sup>63</sup> Monga aja amene anabwera kuchokera ku Emausi, iwo anayenda ndi Iye tsiku lonse ndipo izo zinalepheretsedwa kwa iwo. Ndipo iwo anamuwona mwamuna pa gombe nthawi ina akuwedza pamene iwo anali atawedza; Iye anati, “Ananu, kodi inu mwagwira kalikonse?”

Ndipo iwo anati, “Ife sitinagwire kalikonse, tavutikira usiku wonse .”

Iye anati, “Ponyerani ku mbali inayo.” Ndipo iye anagwira apo gulu lonse la nsomba, ndipo iwo anadziwa pamenepo kuti anali Ambuye. Ine ndikuganiza kuti sanali mawonekedwe Ake amene anasintha, ine ndikuganiza kuti anali maso a anthu chabe amene ankalepheretsedwa.

**385. M’bale Branham, pali kusiyana kwanji, ng—ngati kulipo, pakati pa Mngelo wa Ambuye ndi Ambuye, Mwiniwake.**

<sup>64</sup> Mngelo wa Ambuye ndi mthenga wochokera kwa Ambuye, ndipo Ambuye Mwiniwake ndiye Munthu ameneyo, osati umunthu wa mngeloyo, mngelo wochokera kwa Ambuye. Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu. Kuyankhula kwa mwapansi pano uyu ndi mngelo wochokera kwa Ambuye. Kuyankhula kwa mwapansi uyu ndi mngelo wochokera kwa Ambuye. Kuyankhula za pansu pano apa pali mngelo wochokera kwa Ambuye. Ife tingadziwe bwanji ndiye kuti iwo ndi angelo ochokera kwa Ambuye? Pamene iwo amabweretsa Mawu a Ambuye. Koma pamene iwo ayesera kuti aziwapotoza Iwo, izo si zochokera kwa Ambuye ndiye, mukuona, mukuona, kuyesera kuti awapangitse Iwo kuti anene chinachake chimene Iwo asali kunena. Kumangonena chirichonse. . .

<sup>65</sup> Ndiye pali Mngelo wauzimu amene amabwera pansu kuchokera kwa Ambuye, Mthenga monga Gabrielo, n—ndi Mikaele, Wuduwomu, ndi ena otero, maina awo.

**386. M’bale Branham, chikuwoneka kuti ndi cholakwika nchiyani mu tsiku limene ife tikukhalamo, pokhala wokhulupirira ndipo tikutsatira Uthenga ndi mthenga wa lero, pamene iwe sungamawoneke kuti ukupemphera momwe iwe ukadafunira kumatero? Limenelo ndi funso labwino.**

<sup>66</sup> Ine ndikukhulupirira m’bale, mlongo, aliyense amene anafunsa ilo, ndi chifukwa cha zikhalidwe za nthawiwi. Chitsitsimutso chatha. Chitsitsimutso chakhalapo kwa zaka fifitini zina, ndipo sichinayambe chakhalapo mwa kupitirira zaka zitatu. Ine ndikukhulupirira ilo lalandira chitsitsimutso chake chotsiriza. Ndipo ine ndikukhulupirira ndi chifukwa chake iwe sungathe kupemphera ndi kumamverera mu Mzimu momwe iwe unkachitira. Ndi chifukwa chakuti moto wa chitsitsimutso wazima nutha.

**387. M'bale Branham, chonde longosolani momwe munthu amadziwira ngati iye akuganiza maganizo ake omwe, kapena ngati mdierekezi akuika maganizo mu malingaliro ake kuti azimupangitsa iye kuganiza molakwika, makamaka, ngati iwe ukudziwa kuti iwe sukufuna kuti uziganiza zimenezo.**

<sup>67</sup> Ndiye, ngati izo ziri mosiyana kwa Mawu, uko ndi kuganiza kwa mdierekezi. Ngati izo ziri limodzi ndi Mawu, ndi kuganiza kwa Mulungu. Ngati iwo ali malingaliro olakwika, ndi mdierekezi. Ngati iwo ali malingaliro abwino a Mawu ndi a Mulungu, ndi kuganiza kwa Mulungu.

**388. Ngati nkhaniyo ingakhale kuti mdierekezi akuika maganizo mu malingaliro mwako za chinthu chinachake, kodi izo zingati zigonjetsedwe chotani kapena kuchotsedwa umo?**

<sup>68</sup> Tengani mosemphanitsa kumene kwa izo. Ngati mdierekezi akukupangitsani inu kumaganiza k—k—kuti inu muli... Ngati inu mukudziwa kuti inu ndinu Mkhristu, ndipo iye akuyesera kukupangani inu kumaganiza kuti sindinu Mkhristu, zingotengani mosemphanitsa, nkuti, “Ine ndine Mkhristu.” Bola ngati zokuchitikirani zanu zikugwirizana ndi Mawu a Mulungu itini, “Ine ndine Mkhristu.” Chinthu china chirichonse, mwanjira yomweyo.

**Pamene inu muziyankha ili, chonde ndipemphereni ine kuti ndigonjetse izi, pakuti ine sindiri momwe ndikuyenera kukhalira.**

<sup>69</sup> Mulungu apereke kugonjetsa kwanu, aliyense yemwe inu muli. Mulole malingaliro anu angopita mmbuyo momwe kumbali inayo nkuti, “Ine ndine Mkhristu; ine ndine wokhulupirira. Satana, iwe ulibe pogwirira pa ine.”

<sup>70</sup> Kunena moona, ine ndaima pano pomwe tsopano ndikunena chinthu chomwecho, kupewa kuti ndisakomoke pano pa guwa. Ndiko kulondola. Nthawi zinai kapena zisanu ine ndinatsala pang'ono kugwera pa guwapa. Izo ndi zoon. Mulungu akudziwa kuti uko nkulondola.

**389. Pamene munthu azindikira kuti ali ndi kudziwona kuperevera, kapena mtundu wina wa kudziwona, kodi iye angagonjetse motani izi? Kotero, kodi izo zingakhale kuti ngati iye anali mwana yekha izo zinayambitsa ichi koyambirira kwa unyamata wake?**

<sup>71</sup> Tengani ndendende mosiyantsa. Ngati inu nthawizonse mumangofuna mwa njira yanu, ndi kamwana kakang'ono kaja konyang'wa kamene kamafuna kukhala ndi chirichonse mwanjira yake, inu tembenukirani m'mbuyo momwe ndi kupereka chirichonse chimene inu muli nacho mwanjira inayo. Ngati inu muli odzikonda ndipo mumafuna kugwira chirichonse, ndiye yambani kupereka kwa ena zomwe muli nazo. Mukuona?

Zichitani chirichonse... Muzingopita mosephanitsa. Ndiyo njira yogonjetsera chirichonse, ndiye katemera wake.

<sup>72</sup> Inu muli... Mai anga achikulire, akummwera anakonda kunena kuti, “Ubweya ukachoka pa nsana pa galu ndiko kuluma kwabwino.” Ndipo izo zingagwiritsidwe ntchito mwanjira iyi apanso.

**390. M’bale Branham, ndi phindu lanji limene ife tingamawalole ana athu ammateni kutengapo mbali? (Mwati bwanji, ndi... ) Ndi zochitika zanji zimene ana ammateni oyambirira angamayembekeze, angamachite nawo. Ndiponso, ife tizichita motani powathandizira iwo kusankha oyanjana nawo?**

<sup>73</sup> Ziwasungani iwo ndi amzawo Achikhristu utali wonse momwe inu mungathere kutero. Ziwasungani iwo ndi... Ngati ali msungwana, zimungani iye ndi asungwana Achikhristu; anyama Achikhristu, mosinthanitsa. Ngati iye wakula mokwanira kuti azipita ndi anyamata, muwone kuti iye azipitiriza ndi mnyamata wa mtundu woyenera. Muzimuletsa iye kwa mnyamata wina aliyense, kapena mnyamata kwa msungwana. Ngati iye akumapita ndi wosakhulupirira, yeserani kumulimbikitsa iye kuti azipita ndi wokhulupirira, ndi enawo chimodzimidzi. Pangani panyumba panu kukhala pabwino. Muzipanga panyumba panu kukhala pamalo pamene mwana wanu wamkazi kapena wamwamuna asamachite manyazi kubwera ndi amzake pamaso pa bambo ndi mayi awo, ndi kulowa mu nyumba yawoyo; ndi kupapanga panyumbapo kukhala posangalatsa kwambiri kuti iwo azikhala okondwa kukhala panyumba pawo apo.

Huuu, mai, apa pali seveni motsatana. Ine sindipita kuposa maminisi angapo motalikitsirapo.

**391. M’bale Branham, kodi inu mwanenapo posachedwapa zokhudza kuti m’badwo wa mpingo watha, Laodikaya?**

<sup>74</sup> Ayi, ine sindinanene kuti iwo watha. Ngati ine ndinatero, inu simunandimvetsetse ine, kapena ine ndinanena izo molakwitsa. Izo ziri... Uno ndi m’badwo wa mpingo wotsiriza; ndi kutha kwa mibadwo ya mpingo, Laodikaya. Iwo siunathe; pamene iwo uzitha, Mpingo ukhala utapita. Kotero utali wonse pamene Mpingo uli kuno, iwo siunathe. Mwawona?

**392. M’badwo wa mpingo ukutha ndipo wachita mdima, Mkwatibwi waitanidwa, ife talowa kale mu nthawi ya chisautso?**

<sup>75</sup> Ayi, ayi, ayi, inu muli... Ine ndikukhumba kuti ine ndikanangokhala nayo nthawi yochulukirapo pa zimenezo. Mwawona, mwawona? Mkwatibwi, pamene Iye akutengedwa kuchokera kwa mpingo, ndiye m’badwo wa mpingo utha. Laodikaya apita mu chisokonezeko; Mkwatibwi apita ku Ulemerero; ndipo nthawi ya chisautso ikukhazikika umo pa

namwali wogona kwa zaka zitatatu ndi theka pamene Israeli akulandira uneneri wake; ndiye chisautso chikukhazikika umo pa Israeli; ndiyeno pakubwera nkondo ya Armagedoni imene ikuwononga zinthu zonse. Ndiyeno, Mkwatibwi akubwereranso ndi Mkwati kwa zaka chikwi, ulamuliro wa Zakachikwi; zikatha zimenezo pakubwera Chiweruzo chaku Mpandowachifumu Woyera; zikatha zimenezo pakubwera Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano ndi Mzinda Watsopano kubwera pansu kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba. Muyaya ndi nthawi zikulumikizana palimodzi.

**393. Mzimu Woyera wakuuzani inu kuti Malipenga alibe chochita naye Mkwatibwi. Kodi Mbale Zisanu ndi ziwiri ziri nacho chochita chirichonse ndi ife?**

<sup>76</sup> Ine ndidikira ndi kuwona ngati Mzimu Woyera utawulule izo mwa njira imeneyo. Ine sindikudziwa pakali pano.

**394. Kodi mneneri wa Malaki 4 adzakhala iye amene ati adzawaitane kuti atuluke otsalira a Amitundu a pa Chivumbulutso 7:9, ngakhale ziri kuti iwo adutsa mu nthawi ya chisautso?**

<sup>77</sup> Ayi, ayi! Pambuyo pa—Chivumbulutso 7, ndi pamene iye anawona 144,000 akusindikizidwa, ndipo zitachitika zimenezo iye anawona akubwera apo, akubwerera mmbuyo anali chiwerengero chachikulu chija chimene palibe munthu akanatha kuchiwerenga amene anali Mkwatibwi. Adzakhala nawo...M...Malaki 4 adzakhala atatha ndipo Mkwatibwi atatengedwera mmwamba, ndipo...ndiye...gulu ili l—la Eliya ndi Elisha likubwereranso pa dziko lapansi kwa...Mpingo kuti udutse mu nthawi ya chisautso, koma Eliya ndi Elisha sadzakhala ali ndi chochita chirichonse ndi anamwali ogona (awo ndi Amitundu); iwo adzatumizidwa kwa Ayuda okha.

**395. Kodi Mabingu Asanu ndi awiri amene ndiwo zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimene zaululidwa kale? Kodi iwo anaululidwira mu Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, koma ali panobe—koma iwo panobe sali kudziwika kwa ife ngati Mabingu panobe?**

<sup>78</sup> Ayi, iwo anawululidwa mu Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri; ndi zomwe Mabinguwo anachitira. Iwo anali oti aulule...Mabingu Asanu ndi awiri amene anali atayankhula maliwu awo ndipo panalibe mmodzi amene akanadziwa chomwe iwo anali... Yohane anadziwa zomwe iwo anali, koma iye analetsedwa kuti azilembe izo. Iye anati, “Koma mngelo wachisanu ndi chiwiri, mu masiku a kuwomba kwake, zinsinsi zisanu ndi ziwiri za Mabingu Asanu ndi awiri zikanati zidzaululidwe.” Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri ndi mthenga wa M’badwo wa Mpingo Wachisanu ndi chiwiri. Mwawona?

**396. Kodi inu mukukhulupirira kuti nthawiina Mkwatibwi wamng’ono wamoyo adzasonkhana kwinakwake**

**palimodzi ndi kukhala nazo zinthu zonse mofanana, monga anachitira Mkwatibwi woyamba, mwinamwake kusanachitike kudza kwa Ambuye Yesu mu mitambo?**

<sup>79</sup> Tsopano, iwo anandifunsa ine ngati ine ndikukhulupirira zimenezo. Ine sindingathe kuzitsimikizira izo mwa Malemba, koma mwinamwake idzafika nthawi, mwinamwake, ine sindikudziwa. Pakhoza kukhala basi. . . Inu mukuona? Ngati izo zikanatero, izo zikanapereka kuzindikiritsa kwa kuyandikira Kwake pafupi, kukhala choncho. . . Iye anati, “Koma Iye adzadza monga mbala mu usiku.” Mwawona? Iye akubwera kwa. . . Monga bukhu lija limene ine ndinaliwerenga la Juliet. . . Romeo ndi Juliet, Iye akubwera n—ndi kudzatenga napita naye Mkwatibwi Wake usiku. Iye ali kukwatulidwa napita naye mkamphindi, mu kuthwanima kwa diso. Mwawona?

<sup>80</sup> Ndipo izo ndi zokayikitsa kwambiri ngati ziti zidzakhale mwanjira imeneyo, chifukwa Baibulo linati, “Adzakhala ali awiri mu kama; Ine ndidzatenga mmodzi ndi kumusiya mmodzi; ndi awiri ku munda, ndipo ine ndidzatenga mmodzi ndi kusiya mmodzi.” Mukuona? Kotero iwo mwinamwake. . . Kudutsa mdziko, iwo sadzakhala atasonkhana mu malo amodzi kuti akhale ochita zinthu mofanana. Koma magulu aang’ono a iwo adzakhala atamwazikana konse konse padziko lapansi.

<sup>81</sup> Ine ndikukhulupirira, mwinamwake ngati Ambuye alola, ili ndi gulu laling’ono la Iye. Mwinamwake gulu lina laling’ono ku Asia, lina uko ku Germany, lina uko kwinakwakenso. Pamene ine ndinawona masomphenya a Mkwatibwi usiku wina, Iwo anali opangidwa kuchokera ku maiko onse. Mwaona? Kotero Mkwatibwi sadzasonkhana kuchokera pa malo amodzi, Iye adzasonkhanitsidwa kuchokera konse konse mdziko. Ndipo izo zikutitsimikizidwa ndi Mawu, ndipo Mawu sanayambe alakwitsapo. Ndipo mpaka ku nthawi ino, ngakhalenso masomphenya sanayambe alakwitsapo, chifukwa iwo akhala ali molingana ndi Mawu.

**397. Kodi aliyense amene ali ndi ubatizo weniweni woona wa Mzimu Woyera mu ora lino sadzakhala nawo mu mkwatulo wa Mkwatibwi? Kodi inu mungalongosole? Tiuzeni ife chomwe tingakuchitireni inu mwa njira iliyonse pothandizira kupepusa mtolowu.** Tsopano, kodi izo si zokoma? Mukuona?

<sup>82</sup> Ayi, palibe chimene inu mungathe kuchita pakali pano.

<sup>83</sup> Inde, okhulupirira enieni amene anabatizidwa mwa Mzimu Woyera adzakhala ali mwa Mkwatibwi. Inde, iwo anasankhidwa ndipo anaitanidwa atuluke. Namwali wogona analibe mafuta aliyonse. Amene anali nao mafuta anakalowa umo, koma. . .

<sup>84</sup> “Ife tingachite chiani kuti tikupeputseni mtolowu?” Inde, m’bale, mlongo, aliyense amene walembe izi, zindipemphererani ine; ndicho chinthu chopambana choti mungachite. Zikomo

inu. Ine sindikusowa ndalama. Ine... Nzokwanira zimene zimabwera umo kuti zizindisamalira ine. Ndikuthokoza Ambuye pa zimenezo. Ine sindikusowa zovala. Nthawi zambiri anthu amandipatsa ine zovala zanga zimene ine ndimavala. Ndipo amzanga ndi zinthu amandipatsa ine zovala. Ndipo iwo... Ine ndimapeza ndalama zokwanira kuti ndizilidyetsa banja langa; ndizo zonse zimene ife tikuzisowa. Izo zimawoneka... Ndipo inu mungati muzindipempherera ine, chifukwa ine ndithudi ndimasowa thandizo lauzimu.

**398. Izo zikuwoneka pakati pa atumiki a Mawu, kuti ife tiri nako kulemedwa pang'ono kapena tiribe kuti tizipemphera, kuti tizilalikirira, kuti tizisala, kapena pofuna miyoyo yotaika imene ikhoza kukhala ikadali kunjira uko kwinakwake mu dziko. Kodi inu chonde mungatiuze ife zoti tizichita ndi chikhalidwe ichi? Zikomo mochulukwa kwambiri, M'bale Branham, chifukwa cha izi. Ameneyo ayenera kukhala ali mtumiki. Iye sanalembepo dzina lirilonse pa mau awa.**

<sup>85</sup> M'bale... Ine ndiyenera ndiliyankhe ilo pamene ine ndiri wotopa, wolema, ndipo monga, inu mukudziwa, sindikumverera bwino kwambiri, koteri i—ine ndikudalira kuti izo ziyankha funsolo. I—ine ndikukuthokozani inu mochulukwa kwambiri ndipo i—ine ndinaiwala kuti ndi ziti zimene ndimati ndimuyankhe iye.

<sup>86</sup> Alaliki, mtumiki, chifukwa chake ife tikukhala nako kulemedwa uku... tiribe kulemedwa pofuna miyoyo yotaika. Ine ndikukhulupirira kuti n—ndi kusowa kwa chitsitsimutso. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiziyeserabe kumapemphera kwa Mulungu kuti azitipatsa ife kukhudzidwa pofuna miyoyo yotaika mpaka Yesu abwere.

**399. M'bale Branham, kodi inu mumakhulupirira kuti aliyense amene ali nao Mzimu Woyera amalankhula mu malirime? (Ayi!) Ine ndikudziwa kuti inu munanena kuti kuyankhula mu malirime—kuyankhula mu malirime si umboni wa Mzimu Woyera. Ine ndikanati... Akorinto Woyamba 12:30, chonde longosolani. Kodi inu mungapeze Akorinto Woyamba 12:30? Ine ndikuganiza, “Kodi onse amayankhula ndi malirime?” kapena zina zotero; ine sindiri kutsimikiza. Ine ndiyesera kupeza lina pamene iwo akuliyankha ilo.**

**400. M'bale Branham, kodi inu mungafotokoze Yobu 14:21?**

<sup>87</sup> Inde. Yobu 14 ndi, “Ngati munthu afa, kodi iye adzakhala moyo kachiwiri?” O, ngati munthu afa... Yobu, akukamba za chiukitsiro ine ndikuganiza ine ndinali nalo limenelo mmawa wina, si choncho? Kapena kodi izo zinali ku nyumba ya Charlie? Akazi a Cox anali kumeneko kwinakwake. Yobu, iye ankawawona maluwa momwe iwo ankafera ndi kukhala

moyo kachiwiri, koma iye analowa mu nthaka ndipo sakanatha kubwereranso. Ndiyeno izo zinalongosoledwa kwa iye kuti chinachake chinali chitachimwa. Iye ankafuna mkhalapakati pakati pa iye ndi Mulungu, ndiyeno iye anakuwona kudza kwa Ambuye.

<sup>88</sup> Ndi chiyani icho, m'bale? [M'bale Branham ayankhulana ndi m'bale—Mkonzi.] Ine ndikuganiza kuti apo panali pa Akorinto Woyamba 12:30. Eya!

“Kodi onse amayankhula ndi malirime?” Ndi zimene ine ndimaganiza kuti izo zinali, koma ine sindinali wotsimikiza, pokhala nditatopa monga chonchi, koma . . . Ayi! Si onse amene amayankhula ndi malirime; si onse amene amatanthauzira; si onse amene amanena zimenezo. Ndiyeno mutu wotsatira womwe, “Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime a anthu ndi angelo nkukhala ndiribe chikondi, ine si kanthu.” Mukuona? Paulo, mwa kuyankhula kwina, akuwauza iwo, “Kodi onse amayankhula ndi malirime? Ndithudi, iwo satero. Kodi onse amalosera? Ayi. Koma silirani moonamtima mphatso zopambana; komabe ine ndikukusonyezani inu njira yopambana kwambiri.” Mwawona? Si onse amene amayankhula ndi malirime.

**Kodi inu mukhala nawo msonkhano wina wodziwa za mmitima musanapite kwina? Ngati sichoncho, kodi ndi zotheka kukhala ndi zoyankhulana zapatokha?**

Ine ndikudalira kuti inu munatero. Tsopano, ine ndiribe zochulukira kwambiri zinanso. Ndiroleni ine ndingoyesera kuwatenga iwo ngati ine ndingathe kumene.

**401. Ndikukumbukira ndinakumvani inu mukunena za kuona chinthu chomvetsa chisoni cha mngelo . . . cha mphungu ikumenyetsa mapiko ake mu khola, ikulimbana nazo kuti ikhale mfulu. Ine ndiri nao amayi ofunika ali mu chikhalidwe chimenecho. Iwo akhala asakulolezedwa kuti nao ana awo atatu okwatiwa azibwera kunyumbako kwa zaka zitatu, chifukwa iwo Sali kugonjera ku chiphunzitso cha abambo awo. Iwo ndi mlaliki wakuchipembedo. Amayi amafuna kuti aziumva Uthenga wa nthawi yotsiriza uwo, ndipo ine sindingathe ngakhale kuti nditumize kalata nifika kwa iwo. Ndi mpaka pa muyezo wotani kuti iwo azikhala omvera ku izo? Kodi pali chinthu chinanso chimene ine ndingathe kuchichita pambali pa kupemphera?**

<sup>89</sup> Chimenecho chingakhale chinthu chokha chimene ine ndikanachidziwa. Mwamuna wakeyo, pokhala mtumiki, sakumulola iye kumawamva Mawu. Iye akufuna kuti aziwamva Iwo, koma iye sakumuloleza iye kuti aziwamva Iwo, ndipo basi zimupemphererani iye. Ine ndikukhulupirira kuti mkaziyo n—ndi wopulumutsidwa, ndithudi.



**402. M'bale Branham, ngati kuli kotheka kuti munthu akhale wotayika ndi kukathera mu gehena ngati iye akana Kuwala kwa Mawu, ngakhale kuti iye ali nacho chomuchitikira choona cha kulungamitsidwa ndi kuyeretsewa?**

<sup>90</sup> Inde, bwana! Zimenezo ndi zolondola ndendende.

**403. Pamene inu mugwiritsa ntchito manenedwe oti ngati ife sitiri kukhulupirira Mawu, ife tidzakhala olekanitsidwa mwamuyaya kwa Khristu, kodi inu mukutanthauza kuti anamwali opusa adzakhala moyo mwamuyaya, koma iwo adzakhala ali olekanitsidwa kwa Yerusalemu Watsopano kumene Khristu ati azidzakakhala ndi Mkwatibwi? Pano pali iwo amene libane Mzimu Woyera, obadwa mwatsopano monga Lemba limanenera za kubadwa kachiwiri. Ngati kubadwa kwachibadwa kumafunikira madzi, magazi, ndi mzimu, kodi kubadwa kwauzimu sikumafunikira magawo onse atatu a chisomo munthuyo asanabadwe kwenikweni mwatsopano?**

<sup>91</sup> Mwamtheradi, ine ndazilongosola kumene zimenezo mmawa uja, mofanana, pa chinthu chomwecho. Iwe umayenera kukhala nao masiteji onse. Inu ndinu obalidwa ndi Mzimu, monga momwe mwana amabalidwira, mu mimba ya amake, koma sali wobadwa mpakana iwo ataulandira Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Inu mwabadwa ndiye, inu sikuti mwatembenezidwa. Inu muli mu dongosolo la kutembenezidwa mpakana nthawi imeneyo.

<sup>92</sup> Ndi chifukwa chake zinsinsi zonse zazikulu izi sizikanati ziperekedwe kwa Lutera, sizikanati ziperekedwe kwa Wesile, sizikanati ziperekedwe kwa m'badwo umene wangotidutsa ife kumene, m'badwo wa Chipentekosite. Chifukwa? Iyo siinali nthawi yake. Iwo anali oyembekezeredwa. Tsopano, Umunthu wa Khristu, Mwiniwake, Mwana wa munthu (inu mukumvetsa?) akudziulula Yekha mu mnofu waumunthu, izo sizikanati zibwere mpakana pano.

**404. Pamene Zakachikwi ziziyambika, kodi osakhulupirira adzachotsedwa chotani pa dziko lapansi?**

<sup>93</sup> Osakhulupirira adzapita pansu mu nthawi ya chisautso ndi anamwali ogona, ndi ena onse awo (osakhulupirira, ndi anamwali ogona), ndi otsalira a Israeli amene ali oti adzachotsedwepo.

**405. M'bale Branham, pamene zina za...winawake afika pa ine kapena “akaponda pa zala zanga (Ili liyenera kukhala liri labwino.)—akaponda pa zala zanga,” momwe kunena kwachikale kuliri, mkwiyo wanga umakwera; kodi ine ndingachigonjetse bwanji chinthu ichi? Ine ndikudziwa Ambuye ayenera kuchichita icho, koma kodi ine ndingachite chiyani mu mtima mwanga? Ine sindikuchifuna chinthu chimenechi.**

94 Zikometsani kutentha kwanuko ndi pemphero, ndiye zipangani malingaliro anu. Pamenepo...ine sindikulingalira kuti muli anthu ochuluka kwambiri mu chipinda chino amene anali nako konse kupsya mtima kuposa momwe ine ndinaliri poyambirira pomwe. O, i—ine ndinkakhala ndi kamwa yobwanyulidwa nthawizonse. Ndipo i—i—ine ndinkadya chakudya changa chambiri kupyolera mu kabango.

95 Amayi anga, monga inu mukudziwa, anali theka Mmwenye, ndipo bambo anga anali bambo wachi Irish, wachi Irish waku Kentucky pamenepo. Ndipo wina aliyense wa...Onse a iwo anali ndi kupsya mtima kokwanira koti akanakhoza kumenyana ndi macheka. Ndipo nthawi zonse kamwa yanga inkakhala yosanthidwa; ine ndinali wang'ono pa kuyamba pomwe. Ndipo iwo ankangochita kundinyamulira ine mmwamba ndi kundigong'onthera ine pansi. Ndipo ine ndinkatha kudzuka aponso; ndipo iwo ankandigwetsera ine pansi mobwereza mpakana ine ndinkangokhala wakutha kwambiri...wosatha kuti ndingadzuke apo kenanso. Zimenezo zinali nthawizonse. Ndiyeno pamene ine ndinali wakuti ndingathe kudzuka, ine ndinkadzuka apo kachiwiri; iwo ankandigong'onthera ine pansi mobwereza. Koteru umu ndi mmene ine ndinkakhalira nazo izo.

96 Ine ndinkaganiza, “Ine sindingathe konse kukhala Mkristu.” Koma pamene Mzimu Woyera unabwera mu moyo wanga, izo zinachita icho. Palibenso...

97 Ine ndinali ndi mzimai nthawi ina; ine ndinapita kuti ndikaduleko magetsi. Ndipo tsiku limenelo ine ndinali ndi tsitsi pamwamba pa mutu panga. Iye anati, “Iwe wamng'ono, wa tsitsi lopiringika wauchitsiru!”

Ine ndinamuza iye, ine ndinati, “Mzimai, iwe sukuyenera kumatukwana monga choncho. O, kodi iwe sumawopa Mulungu?”

Iye anati, “Iwe wamng'ono, wa tsitsi lopiringika wauchitsiru, ngati ine ndikanafuna winawake woti ayankhule kwa ine za zinthu monga zimenezo, ine sindikanati nditenge wa nyonga zatheka ngati iwe.”

“Huu!” Ndiye iye ananditcha ine dzina la *mkabudula, kabudula*. O, mai, ngati zimenezo zikanakhala ziri chaka chapataliko! Ine nthawizonse ndinkati, “Mwamuna amene angamuwombe mkazi si mwamuna wokwanira kuti angamuwombe mwamuna,” koma i—ine mwina ndikanaziswa zimenezo pa nthawi imeneyo atawatchula amayi anga dzina loipa ngati limenelo. Koma inu mukudziwa chiyani? Zimenezo sizinanditututse nkomwe ngakhale ine. Ine ndinati, “Ine ndikakupemphererani inu.” Sizinandivutitse konse...Ine ndinadziwa apo pomwe kuti chinachake chinali chitachitika kwa ine. Inde, bwana! O, mai!

<sup>98</sup> Inu mukudziwa zoyipa zimene ine ndinkazichita pamene ine ndinali mwana, kumenyana! Ine ndinat sala pafupi kupha amuna asanu pa nthawi imodzi. Ndinatenga mfuti yodzaza ndi zipolopolo sikisitini, ndipo pamene anyamata amenewo anandimenya ine chifukwa ine ndinali wachi Kentucky, popanda chifukwa china. . . Ine sindinkatha ngakhale kukweza mutu wanga mmwamba. Wina anali kundigwira ine pa dzanja monga chonchi, ndipo wina ankakhoza kuima pamenepo ali ndi mwala mdzanja lake ndi kundisantha ine mu nkhope, mpakana ine ndinangokhala wopanda moyo. Palibe kanthu mu dziko. . .

<sup>99</sup> Iwo ankanditcha ine “wosakanizika ndi chimwenye waku Kentucky,” chifukwa amayi anga, pamene iwo anali aang’ono, iwo ndithudi ankawoneka ngati Mmwenye (ndimayang’ana pa chithunzi chawo kanthawi kapitako), ndipo iwo ankadziwa kuti iwo anali Mmwenye mwatheka. Ndipo chifukwa ine ndinali waku Kentucky ndipo iwo pokhala mkazi wosakanizika ndi chimwenye, iwo ankanditcha ine “wosakanizika ndi chimwenye, wosakanizika mitundu waku Kentucky.” Ndipo ine ndinalibe kanthu mu dziko koti ndichitepo pa izo; ine sindikanatha kuchitira mwina chifukwa ine ndinabadwira ku Kentucky.

<sup>100</sup> Ine ndinkapita kumusi uko ku sukulu, ndipo ine ndinalibe zovala zoti ndizivala, ndi tsitsi langa likulendewera pansu pakhosi langa. Ndipo Agogo. . . Amayi anatenga chikhotho chakale cha Agogo chimene iwo anakwatira atachivala, ndipo anachidula icho ndipo anandipangira ine tharauza loti ndizivala ku sukulu nthawi yanga yoyamba. Ndipo ine. . . ndipo iwo anandiveka ine masitonkeni oyera ndi nsapato za tenisi. Ndipo iwo ankati, “Ngati iwe usakuwoneka ngati ‘wopepeka’ waku Kentucky.” N—ndi zonse—ndipo izo—ndiyeno, izo zimapitirira choncho yonse—masiku a sukulu anga onse.

<sup>101</sup> Ndipo anyamata angapo, chifukwa ine ndinkayenda mu msewu ndi mtsikana wina wamng’ono ndipo ndinanyamula mabuku ake. . . Iwo sankafuna kuti ine ndizichita zimenezo, ndipo iwo anakomana nane ine kumusi uko ndipo anandimenya ine mpakana ine ndinali nditakomoka basi. Ine ndinawauza iwo, ngati iwo akanangondilola ine kuti ndizipita, ine ndinalonjeza kuti ine ndikanapita molunjika kwathu. Ndipo koteri iwo anatenga. . . anandisiya ine, anandimenya ine kanai kapena kasanu, anandigwetsera ine pansu, ndipo anaikanda nkhope yanga yonse. Ndipo ine ndinapita kwathu, monga choncho, kukwera kudutsa mmunda wa tchire la masache.

<sup>102</sup> Ine ndinali ndi mfuti yaing’ono ya .22 Winchester ili cha pa khomo. Ndinafikira pamwambapo ndipo ndinaidzazitsa mfuti imeneyo ndi zipolopolo, ndinapita uko komwe kudutsa mu ziyangoyango za dzombe, ndipo ndinabisala mmphepete mwa msewu mpakana anyamata asanu awa kapena asanu ndi mmodzi anabwera motsatira kumeneko. Ine ndinangodikirira mpaka iwo abwere, ndipo pamene iwo anali kubwera pamenepo,

akuyankhula, ankati, “Wachi Kentucky uja azindikira kumene iye ali kuchokera apa mpakana,” kumapitiriza nazo monga choncho

<sup>103</sup> Ine ndinatulukira apo nditakoka kokhwefulira pa mfutiyo. Ine ndinati, “Tsopano, ndi ndani wa inu amene akufuna kuti ayambirire kufa, chotero kuti iwe usawawone amzakowo?” Iwo anayamba kukuwa; ine ndinati, “Musati mukuwe, chifukwa inu nonse mufa mmodzi ndi mmodzi.” Ndipo ine ndinkanthauza zimenezo! Ndipo apo pomwe iwo anayamba kukuwa. Ndipo ine ndinaikoka iyo ndipo ndinaiwomba! Mfutiyo inakanirira. Ine ndinaponyera umo chipoloplo china. Kuwomba iyo, icho chinakanirira; chipololo china, kuwomba, icho chinakanirira. Ndipo ine ndinapopera zipolopolo sikisitini pansi. Chirichonse cha izo chimakanirira. Ndipo anyamata amenewo akuthamanga, ndi kukuwa, ndipo akulumphira pa phiri, ndi chirichonse.

<sup>104</sup> Ndipo iwo atachoka kale, ine ndinaima pamenepo. Pamene ine ndinkakhala nditakwiya kwambiri, mpaka i—i—ine sindinkatha kulira, ine ndinkaseka ngati chitsiru ndi misonzi ikutsikira mmaso mwanga. Tsopano, kumeneko ndiko kupsya mtima. Ngati akanati asakhalepo Mulungu, ine bwenzi ndiri wakupha.

<sup>105</sup> Ndipo ine ndinatolera zipolopolo zimenezo ndi kuzibwezera izo mu mfutiyo, ndipo, “Pho, pho”; izo zinkawombera bwino bwino basi monga nthawizonse. Kukamba za chisomo!

**406. Kodi anamwali opusa alikuti mu nthawi ya Zakachikwi?**

<sup>106</sup> Mu Zakachikwi iwo ali mmanda. “Okufa onse sanakhale moyo kwa zaka chikwi.”

**407. Kodi uko kudzakhala, kapena kodi kuli tsopano malo oti Mkwatibwi asonkhanireko palimodzi kuti azikakhala, monga pamene Mose ankatsofolera ana a Israeli?**

<sup>107</sup> Ine ndikuyankhani inu funso limenelo; izo zangowululidwira kwa ine. Ine ndikuuzani inu choonadi. Inde, bwana! Pali malo a Mkwatibwi yense kuti asonkhane. Kodi inu mukufuna kuti mudziwe komwe iwo ali? Mwa Khristu. Kulondola. Zingomasonkhanani mmenemo; ife tiri tonse palimodzi?

**408. Chifukwa chiyani kuti ife timaitenga kukhala nkhani yaikulu ya kavalidwe ka akazi (O, o, ine ndikuzilandira izo pa ili, sichoncho ine?)—nkhani yaikulu pa kavalidwe ka akazi ndi kudula kwa tsitsi, ndi kuchita...popanda kanthu konenedwa za tsitsi la mwamuna kapena momwe iye amavalira?**

<sup>108</sup> Chabwino, mlongo, ine ndati ndigwirizane nanu pa chinthu chimodzi. Malo oyambirira, Baibulo limanena kuti mwamuna asamakhale ndi tsitsi lalitali. Ndipo ngati iye akanakhala ndi tsitsi lalitali, ine ndikanamuuza iye, chimodzimodzi momwe ine ndikukuuzirani inu. Iye akulakwitsa. Koma amuna ambiri,

ochulukuka a iwo ngati ine, alibe lirilonse nkomwe. Koma amuna ambiri amadula tsitsi lawo, amawoneka ngati amuna. Ndipo tsopano, ngati iwo akanati asamachite zimenezo, iwo akanati aziuzidwa kuti asamachite choncho, kusiya tsitsi lawo likukula ngati tsitsi la mkazi. Inu mudzazipeza zonse izi mu malumbiriro a chikwati ndi chilekano ndi zinthu pamene ife tizidzalalikira pa izo. Nkhani yaikulu monga ngati ya mwamuna... kapena kavalidwe ka mkazi...

<sup>109</sup> Tsopano, mwamuna, malo oyamba, thupi la mwamuna si liri yesero monga la mkazi. Tsopano, mwamuna, iye ndi wamkulu, wokalamba, ali ndi miyendo yaubweya, maondo-ogundana, mimba ngati mphika, ndi chirichonse, iye ndi chisokonezeko chosawoneka moipa; ndipo palibe kanthu pa iye ka yesero. Ndipo ine ndikuganiza iye amawoneka mawonekedwe “onyansitsitsa” kwa maso kuti umuwone mwamuna uyu akubwera mu msewu, wamng’ono kapena wachikulire, atavala akabudula osambira nao awa, chirichonse chimene icho chiri, inu mukudziwa, kumayenda akubwera mu msewu. Ine ndikuganiza kuti amenewo ndi mawonekedwe onyansitsitsa kwambiri ine ndinayamba ndayang’anapo. Ndiko kulondola. Ine ndikuganiza i—iye sakudziwa mbali ya mtundu imene iye ali wa iwo (mukuona? Uko nkulondola!), mwamuna amene angachite chinthu ngati chimenecho.

<sup>110</sup> Ndipo inu mukudziwa chiani? Ine ndamva kumene miyezi ingapo yapitayo, Ankhondo Achimereka akuti azivala mwanjira imeneyo. Eya! Ankhondo amene akubwerapo chaka chamawa, kapena chaka chikatha chotsatirachi, onse mu makabudula. Ife tingafike motani pokhala gulu lachikazi lalikulu?

<sup>111</sup> Mulungu anamupanga mwamuna kuti aziwoneka monga mwamuna, ndi kuti azichita monga mwamuna, ndi kumavala monga mwamuna. Iye anamupanga mkazi kuti azichita chimodzimidzi, azivala monga mkazi, azichita monga mkazi, ndi kukhala monga mkazi. Pafupi mmawa uja...za... Funso linabwera lokhudza mwamuna... [Mbali imodzi ya tepi itha mosathetsetsa ndipo mbali yachiwiri ikuyamba mosakwanira—Mkonzi.]... Ngati iye akufuna kuti...

<sup>112</sup> Ngati mkazi ali ndi tsitsi lopyapyala kwenikweni, ndipo iye akufuna kuti azivala imodzi ya “makoswe” awo kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho, ine ndikuganiza ndizo... Akazi anga amachivala icho. Ndi... Iwo amati tsitsi lawo ndi lopyapyala, ndipo iwo ali ndi chinthu cha mtundu wina pafupi chachikulu choncho, chimawoneka ngati sikono yaikulu kwambiri, yopitirira muyezo. Ndipo iye amakulunga tsitsi lake mozunguliza icho namanga ndi mapini mmenemo. Ndipo tsopano, a... Monga momwe ine ndikudziwira, i—izo sizimavutitsa chirichonse bola ngati tsitsi lanu liri lalitali.

113 Mtumiki anati mkazi wake a—anali kutsutsika, chifukwa iye anali—utoto mu tsitsi lake. Ndipo ine ndinapeza kuchokera pa funsolo, izo zikutanthauza utoto kapena kulocha mu tsitsi lake. Ine sindingati ndinene kuti izo ndi zolakwika; ine ndiribe kanthu pa izo. Ngati iye ali ndi tsitsi lalitali, ndi zokhazo zimene ine ndingathe kunena pa ilo.

114 Ndipo tsopano, mwamuna . . . Munthu uyu anati mmawa uja za kulichotsa tsitsi lawo, kulivalanso ilo. Tsopano, izi zinakhala ngati zafikanso apa, za kudula tsitsi. Mukuona?

115 Tsopano, ng—ngati mwamuna alibe tsitsi, ndipo mkazi wake. . . Ine ndawamvapo akazi akuti, “Chabwino, ngati ine ndikanangomupezera John. . . Ine ndikuganiza iye akanati aziwoneka bwinoko ngati i—ngati iye akanamavala kachidutswa ka tsitsi. Kodi inu mukuganiza chiani pa izo, M'bale Branham? Kodi izo ndi zolakwika kuti iyeyo achite zimenezo? Ayi, bwana! Ayi, ndithudi, izo si zolakwika, osati konse. Ngati iye akufuna kuti azilivala ilo, zimenezo ziri bwino, sizikuposa monga kuvala mano oikirira kapena chirichonse chimene chingabwere pamenepo.

116 Tiri chiyankhulire, ine ndiri nawo mano atatu oyikirira inemwini. Ine ndikukhumba ine ndikanati ndisakhale nawo iwo. Iwo ali pa waya; iwo nthawizonse amafupikitsa liwu langa, ndipo amadula lirime langa, ndi china chirichonse, koma ine ndikuyenera kuti ndikhale nawo iwo kuti ndizidya. Ndipo ngati ine. . . pamene ine ndiri kutsidya kwa nyanja ku misonkhano ya kunjja iyo, ine ndimavala kachidutswa ka tsitsi; osati chifukwa cha mawonekedwe ake, chifukwa inu mukudziwa ine ndikanakhoza kuima pano pomwe ngati ine ndikanakhala ndiribe tsitsi pamwamba pa mutu wanga kapena chirichonse chimene icho chinali. Sizikanapanga kwa ine chosiyana ayi; ine ndiri pano kuti ndidzamuimire Yesu Khristu. Koma pamene ine ndimaima kunjja uko, pafupi usiku woyamba mu umodzi wa mikuntho ya kotantha uko, usiku wotsatira mmero wanga umakhala uli wotupa kwambiri ine sindimatha kupita kunjja uko.

117 Koterono, ng—ngati chikanakhala chinachake chimene ine ndimafuna kuti ndichite icho, ndipo ine ndikulephera kuti ndichite icho, ine ndikanachita icho. Inde, bwana! Palibe chinthu chimene chimanena kuti ayi musamachite icho. Palibe chinthu chimene chimanena kuti, mlongo, kuti inu simungavale khoswe, kapena tsitsi lovala, kapena chinachake kapena chimzake mu lanu. . . Zimenezo ndi zabwino mwangwiwo, koma zilolani tsitsi lanulo lizikhala likanali lalitali. Ndipo amuna, inu muzidula tsitsi lanu. Limene inu muli nalolo, muzilisunga ilo litadulidwa. Mukuona? Ndiye, izo zikukhazikitsa icho.

118 Ndipo akazi, inu muzivala ngati akazi. Ndipo amuna, inu muzivala ngati mwamuna; musati muziyesera kumakhala ngati

wachikazi ndi kumavala zovala za akazi. Ndipo akazi, musati inu muziyesera kukhala mwachimuna ndi kumavala zovala za amuna, chifukwa Mulungu sakufuna kuti inu muzichita zimenezo; Baibulo limatsutsa zimenezo.

<sup>119</sup> Koma tsopano, za kuvala chidutswa cha tsitsi kapena kuvala tsitsi... Chabwino, kodi ndi chiani chimodzi cha izo “makoswe”? Kodi ine ndinalakwitsa kanthawi kapitako kapena kodi imeneyo ndi “mbewa”? N—ndi chinachake—ndi chinachake chimene—mkazi amaika mu tsitsi lake kuti ilo liziwoneka lochuluka... Chirichonse chimene icho chiri (mukuona?), palibe kanthu kolakwika ndi zimenezo. Pitirirani nazo, ziri bwino.

**409. M’bale Branham, mlongo anabwera ku kachisiyu mailosi eyiti handiredi, ndipo iye anati iye akukhulupirira kuti inu ndinu Yesu Khristu mu thupi. Chonde yankhulani pa izi. Iye anali (w-o-s-a-...) wosadzigwira poyesera kumawauza ena zomwe iye akuganiza. (W-o-s-a-d-z-i-g-...) wosadzigwira. Chabwino.**

<sup>120</sup> Tsopano, ndithudi mlongoyo anali kulakwitsa. Ine si Yesu Khristu; ine ndine wantchito Wake. Ife tadutsa mu zimenezo nthawi zochulukira kwambiri. Koma...

O, ine ndikuyandikira kwambiri tsopano; mungondipempherera ine, tipitiriza mochepa pang’ono pokha.

**410. M’bale Branham...** (Kodi inu mungafune kuti muwamve ena onse a iwo—mofulumira momwe ife tingathere?) **M’bale Branham, nthawi ina ine ndinalephra Mulungu anandipatsa ine...ndikumverera Mulungu anandipatsa ine lonjezo monga ngati Sarah. Panali funso, koma lonjezo linabwera pambuyo pake. Kodi lonjezolo linali la Mulungu? Ine ndimadziwa chomwe la Sarah linali, koma ine ndikumverera kuti nthawi yafupika kwambiri. Ife tikuukonda utumiki wanu ndi Iye amene anakuitanirani inu kwa iwo (Izo ndi zokoma, sichoncho izo?)—tikuukonda utumiki wanu ndi Iye amene anakuitanirani inu kwa iwo, ndipo chotero, ife timakukondani inu. O, iwo analembapo dzina lawo. Zikomo inu, mlongo ndi m’bale. Funso, eya, eya, chabwino.**

<sup>121</sup> Tsopano, Mulungu...Ndikuganiza Iye anakupatsani inu lonjezo, ndipo izo zinachitika monga Sarah. Zedi, ndi Mulungu yemweyo; Iye amayankha mwanjira yomweyo. Inu musati mukhulupirire zina zakenso koma izo zinali za Mulungu.

**M’bale Branham, ine ndikanafuna kuti ndikufunseni inu mafunso ena okhudza Baibulo. Chonde talongosolani Marko Woyera...**

Ine ndinali nalo ilo; ine ndinali nalo ilo, Marko Woyera 16. Ife tinawerenga zimenezo tsiku lina, ine ndikukumbukira, tiyeni tiwone.

**411. Wokonedwa M'bale Branham, chonde talongosolani Mateyu Woyera mutu 22, ndime, pamene . . .** (Ife tinalitenga limenelo. Mwawona? Mukukumbukira tsiku lina lija? Ine ndi—ine ndisonyeza izo kwa inu. Ine ndina . . . Ziwoneni izo apa pomwe, 22.) **Kodi mlendo uyu anadzalowa bwanji mu Mgonero wa Chikwati, amene anali atavala chovala, koma iye sanavale chimodzi cha zovala zaukwati?**

<sup>122</sup> Mukukumbukira, ine ndinati. . . Ine ndinakhala ngati ndakokerapo nthabwala yaing'ono; ine ndinati, "M'bale wa chipembedzo amene anadza pa—a . . . anadzera pa zenera ndipo osati kudzera pa Khomo." Khomo ndi Mawu.

**Inu munanena kuti Kaini anali wa mbewu ya serpenti. Nchifukwa chiani Eva anati, "Ine ndalandira munthu kuchokera kwa Ambuye"?**

Ilo ndi limene ine ndimayesera kuti ndilipeze mmawa uja. Ine ndiri ndi Malemba ndawalemba apa a zimenezo. Ine ndikhoza mwina kubwerera mmbuyo pang'ono; ine ndikuyembekeza choncho. Ndikupeza ena apa . . .

**M'bale Branham, amuna anga, amene analedwa mu Chikatolika, mu kupembedza kwathu iwo akufuna azipemphera mwa njira yawo.**

Ine ndinali nalo limenelo. Mukukumbukira?

O, ine ndikuzipeza izi apa pomwe tsopano. Ine ndinali nazo zimenezo.

**M'bale Branham, ine potsiriza . . . kuti ndimusangalatse mlongo wanga wochokera ku chi- . . .** Ine ndinali nalo ilo. Dona anali ndi mlongo wake wa Chikatolika.

**M'bale Branham, mu II Timoteo 4, mphatsoyo ndi chiani imene inaperekedwa kudzera . . .**

Ine ndinali nalo ilo. Ndi angati amene akuwakumbukira awo? Ine ndiri nawo ena a iwo atasakanizidwa apa? Mwawona?

**Kodi ndi kololedwa kuti ife tizigwiritsa ntchito mtundu uliwonse . . .**

<sup>123</sup> Uko ndi kuteteza kubala. I—ine . . . Ndiroleni ine ndiyankhulane kwa inu pa—padera pa zimenezo (mwawona?), monga ine ndinanenera mmawa uja.

**Loyamba, kodi anamwali opusa asanu anapulumuka nthawi ya . . .**

Ine ndinali nalo ilo. Ine ndikubwerera apa. Miniti yokha, ingokhalani opilira nane.

**Titatha kudziwa njira, bola njira ya kulapa ndi kuyeretsedwa** (ine ndinali nalo limenelo, inu mukukumbukira?), **ndiye nkugwera kutali kwa icho . . .**

Ine ndinali nalo ilonso. Ine ndabwerera mmbuyo mwanjira ina. Ine ndiyenera ndingowatenga iwo momwe . . .



**M'bale Branham, tanthauzo lake nchiani la Mateyu Woyera 24:28: “Pakuti kulikonse kumene kwafa nyama, kumeneko mphungu zikasonkhanira”?**

Mukukumbukira ine ndikulungosola zimenezo? Mwaona? Ine ndinali nazo zimenezo. Mwinamwake ine ndazitsiriza izi. Ambuye alemekezeke!

**Ndi nthawi—kodi iyi ndi nthawi yoti Mkwatibwi ayenera k—kuti akakhale ali ndi inu kwa (Tsopano, ndinali nazo zimenezo.) mkwatulo?**

Mwinamwake ine...Ndipo ine ndikudziwa ine ndinali nazo zimenezo, chifukwa ilo linalembedwa pansu; ine ndikukumbukira zimenezo. Chabwino, Ambuye alemekezeke! Ife tikufika mmusi momwe apa tsopano. Tiyeni tiwone.

**412. Pakuti Machitidwe 2:38 ndiyo njira yokha kuti ubatizidwe, nanga bwanji unyinj. . . ? Ine ndinali nalo limenelo.**

<sup>124</sup> Iwo sankazidziwa izo mu masiku awowo; izo zikungoululidwa tsopano. Inu mutadziwa kale zoti muchite, “Kwa iye amene amadziwa kuchita molondola ndi kusachita izo, kwa iye liri tchimo.”

**413. M'bale Branham, kodi ndi zolakwika kulima—kulima ndi kugwira ntchito mu fodya? Ine sindikukhulupirira kuti ine ndinali nalo ilo.**

<sup>125</sup> Tsopano, ine ndimatsutsana naye fodya. Ine ndimatsutsana nako kugwiritsa ntchito kwa fodya; Mkhristu aliyense wobadwa kachiwiri angatero; ndizo zonse, chifukwa ndi zolakwika. Ife tikudziwa kuti ngakhale asayansi yamankhala amanena kuti ndi zimene zimayambitsa zochuluka za khansa yapammero n—ndi ya mmapapu, n—ndi fodya. Iwo amati, “Muzisuta ndudu zosefedwa.”

<sup>126</sup> Tsopano, kwa inu amuna ndi akazi amene mumasuta, kumeneko ndi kukunyangani chabe inu, chifukwa inu simungati...Chabwino, chinthu chokha chimene iwo amachita...Pamene inu mugula ndudu zokhala ndi sefa, inu mumayenera kuti mugule zambiri za izo, chifukwa iyo imangololeza kagawo kenakake ka utsi kuti kazidutsa. Chifukwa aliyense angakuuzeni inu. . .

<sup>127</sup> Ine ndinamumva mphunzitsi uja ku Chiwonetsero cha Mdziko uko mu Washington chaka chatha (pamene ine ndinali kumeneko ku Chiwonetsero cha Mdziko), ndipo madokotala amenewo ochokera konsekonse mdziko uko analongosola izo; ananena kuti iwe sungakhale nao utsi wopanda chikonga, ndipo iwe sungati...Ndipo ngati iwe uli ndi utsi iwe uli nacho chikonga. Ndipo anati, “Musati mumulole munthu wina akunyengezeni inu pa ndudu zokhala ndi sefa, pakuti pamene inu mukanasuta imodzi kapena ina imene ikanakhutitsa chibaba chimene inu muli nacho pa ndudu, inu muzisuta ziwiri

kapena zitatu za zinazo.” Ndi machenjerero chabe—apagulu, machenjerero a kulengezera pa wailesi ndi televizioni.

<sup>128</sup> Koma kugwira ntchito mu fodya kapena kulima fodya. Tsopano, inu abale aku Kentucky amene mumalima fodya uyu... Chabwino, ndiroleni ine ndinene chinthu chimodzi: Ngati izo zimakutsutsani inu pakuchita zimenezo, inu musati muzichita zimenezo, chifukwa ine sindikanafuna kupanga chinachake chimene chikanati... chimene ine ndikudziwa kuti chinali kumuthandizira winawakenso ku imfa yake. Ndi zolakwika kumupatsa woyandikana naye chakumwa chaukali, ndiye izo zingakhale zolakwika kupanga chakumwa chaukali. Koma ndiroleni ine ndinene chinachakenso tsopano. Tsopano, tikanena za kumulima iye... .

<sup>129</sup> Fodya, inu mukudziwa, nikotini amagwiritsidwa ntchito ndiponso mu njira zamankhwala. Ndipo kodi inu mumadziwa kuti inu mumalima chimanga chimene amapangira mowa, tirigu ndi balere amene amapangira mowa? Uko nkulondola? Chabwino. Mwawona? Inu simungadziwe chomwe iwo akanati akamugwiritsire ntchito iye.

<sup>130</sup> Koma tsopano, ife timalima chimanga, kuti ife tingathe kulingalira pamene ife tikulima chimanga, kuti icho akapangira makonifulekisi, ndi chakudya cha anthu, nsima ya chimanga, ndi zina zotero; koma iwo amapangira aponso zakumwa zoledzeretsa kuchokera mwa icho (mwawona?), kotero iwe sungadziwe choti uchite.

<sup>131</sup> Ndipo inu mumalima... Inu mukakhala ndi munda wa kakombo. Inu mukudziwa zomwe iwo amachita ndi kakombo? Iwo amapangira opiamu kuchokera mwa iye. Inu mukudziwa zomwe iwo amachita naye letesi? Iwo amachita naye chinthu chomwecho. Opiamu alimonso mu letesi. Kodi inu munayamba mwadyapo letesi wambiri ndi kuwona mmene mumafatsira kwa kanthawi pang’ono? Ndi opiamu amene ali mmenemo. Kodi inu mukudziwa kuti iye alinso mu anyezi? Zedi. Kotero, i—inu mukuona, zimatengera pa zomwe inu mukuchita naye iye.

<sup>132</sup> Koma ndiroleni ine ndinene izi, monga m’bale wa Chikhristu kwa m’bale wa Chikhristu: Ngati inu muli ndi munda wa fodya, ugulitseni iwo kwa winawake, yesani mwayi wanu pa chimanga. Ine ndikukhulupirira kuti izo zingakhale zabwinoko (mwawona?), chifukwa palibe kukayika pa chimene iwo akumulimira iye... .

### **Mwamuna wanga anakwatirapo chidakhwa ndi wachigololo... .**

Ine ndinali nazo zimenezo. Zabwera kuchokera... ine ndinakuuzani inu kumene izo zikuchokera. Izo ndi zochokera kutali ndi kuno. Ine ndinali nalo funso limenelo. Ndipo tsopano, tiyeni tiwone.

### **Mkazi wa pa Chivumbulutso 12... .**

Ine ndinali nalo limenelo. Eya, ine ndiri nawo mulu uwu wa mafunso. Tiyeni tiwone. Izo ndinali nazo; ine ndinali nazo izo. Ndi pa Chivumbulutso 12, chimene iye anali. Tiyeni tiwone.

**414. M'bale Branham, ife tiri ndi ana awiri amene amapita ku mpingo umene umatsogoleredwa ndi mlaliki wa chikazi. Ife tikudziwa kuti iye ali kunja kwa Mawu. Ana athu ali pansu pa kukopa kwamphamvu uku. Kodi ife tichite motani powauza iwo kuti uku ndi kulakwitsa?**

<sup>133</sup> Ine ndinakuuzani inu kale. Ine ndinaliyankha limenelo. Ndipo mukazichite izo modekha. Inu mukananena chiyani ngati ine. . . Ine ndikudziwa munthu ameneyo ali pano. Inu munganene chiyani ngati ine ndikukhulupirira kuti ine ndikumudziwa yemwe mkaziyo ali ndipo ine nditha kukuuzani inu?

**415. Kodi ulamuliro wa Zakachikwi udzakhala zaka chikwi chimodzi kapena ndi kawerengedwe ka nthawi chabe?**

<sup>134</sup> Ine ndinali nalo limenelo ngakhale mmawa uja. Mwawona? Ndi zaka chikwi. Chabwino.

**M'bale Branham, vuto la chomwe. . .**

Eya, ine ndinali nalo ilo. Tirigu ndi namsongole, inu mukukumbukira ife tinali nazo izo.

Ine ndikukhulupirira ife tikufika pansu pomwe tsopano. Ine mwina ndinaponyera mulu wa izi mmbuyo. Tiyeni tiwone. Chinthu chomwecho.

**M'bale Branham, ine ndine mayi wa ana asanu ndi mmodzi odabwitsa ndipo mwamuna wanga akufuna kuti ine ndipite ku kagwira ntchito kwa kanthawi kuti ndimuthandize pachuma. Kodi ine nditero? Inenso ndikufuna kuti ndipemphere kwa Mulungu kuti andipatse ine chikhulupiriro kuti. . . kuti andipatse ine. . . Abrahamu n—ndi. . . monga. . . chikhulupiriro chofanana. . . monga Abrahamu ndi Daniele ndi ana Achihebri. Kodi Mkristu azilima fodya? Ine ndadutsa kumene mu zimenezo. Ndipo. . .**

**416. M'bale Branham, kodi ndi zolakwika kuti mkazi azimeta miyendo yake?**

<sup>135</sup> Kodi ine ndikuwona zinthu? Kodi ilo likunena zimenezo? Ine sindingathe. . . ine sindikanadziwa. Ine ndisiyira zimenezo kwa inu.

**K—kodi lero ndi zolakwika kuchepetsa banja lako? Kodi izo zikutanthauza kuteteza kubala kwathunthu?**

<sup>136</sup> Ine ndinayankha zimenezo, ndithudi, kwa. . . wina aliyense. Tiyeni tiwone.

**Ngati mkazi akanali mu tchimo atenga chisudzulo ndi kukwatiranso ndi. . .**

<sup>137</sup> Ine ndinaliyankha limenelo. Inu mukukumbukira ine ndinati, “Isiyeni nkhani ya chilekanoyo mpakana . . .”

**417. Ine ndiri ndi mzanga amene ine ndimamukonda kwambiri. Iye wakhalapo nao matepi ena ndi makalata amene ine ndikukhulupirira kuti ali... sindinayambe ndalankhulanapo kwa iye. Kwenikweni, ine ndikupenekera kuti ine ndikuopa kuti ndingamuwononge iye ndi kumutaya iye ngati wapaubwenzi. Kodi ine ndichite chiani?**

<sup>138</sup> Yankhulani kwa iye mwa chikondi. Ine sindiri...Ine ndikukhulupirira ine ndinaliyankha limenelo, koma i—ine ndi...Sindi—sindimayesera kukankhira chirichonse pa aliyense. Zingokhalani amchere; iwo azikhumba kuti akhale monga inu.

M’bale, mlongo, ine ndikukhulupirira ndaliyankha ili.

**M’bale Branham, chonde talongosolani za anamwali opusa asanu.**

I—ine ndikudziwa ine ndinali nalo ilo. Ilo lalembedwa, ndipo ilo ndi pepala lofiira. Ine ndikukhulupirira ife...ine ndinali nalo limenelo. Ine ndikukhulupirira ine ndawayankha onse awa. Ambuye alemekezeke. Tiyeni tione. Ndikhulukireni ine miniti yokha.

**418. Wokonedwa mneneri wa Mulungu, Marko, 16:18, i... gawo la kuyika manja pa odwala . . . Ine ndimakhala pafupi ndi ogwira njoka. Nanga bwanji zimenezo?**

<sup>139</sup> Chabwino, limenelo ndi funso labwino. Ngati inu muli pafupi ndi ogwira njoka, ndipo iwo amati Marko 16... Ndithudi! Ine ndikukhulupirira kuti Baibulo limatanthauza basi zimene Ilo limanena. Ine ndikukhulupirira kuti ngati ife tiyesera kuwayesa Ambuye mu chinachake, ife tipezana nazo. Koma ine sindikuganiza kuti Mulungu akutanthauza kuti inu mundibweretsere ine botolo la chiphe ndi kuti muwone ngati ine ndingazimwe izo ndi kutsimikizira kwa inu kuti ine ndiri nacho chikhulupiriro; palibe choonjezera kuposa kuti ine ndizikhulupirira kuti chingakhale cholondola kuti inu mundibweretsere ine njoka, ndi kundisiya ine kuti ndiitole iyo, ndi kukusonyezani inu kuti ine ndiri nacho chikhulupiriro kuti ine ndikhoza kugonjetsa chiphe chakecho. Ine sindikukhulupirira kuti izo ziri chomwecho.

<sup>140</sup> Ine ndimakhulupirira kuti ngati ine ndikanakhala ndiri mu madzi ndikubatika anthu, kapena kuchita pa ntchito ya Ambuye, kapena kunja mu nkhalango, ndipo njoka ikanandiluma ine, ine ndikanayenda mopitirira kumene mu Dzina la Ambuye. Mukuona? Ine ndikukhulupirira kuti ndi zimene izo zimatanthauza.

141 Tsopano, ngati inu mukanachita kutenga...Mukuona, zimene inu mukuchita ndi izo, munthu wokondedwa yense yemwe inu muli—yemwe inu muli...Kumbukirani izi. Mukuona? Penyani zimene Baibulo linkachita nazo izo. Mosachuluka kuposa momwe ine sindikukhulupirira kuti ngati inu mutayesa kumanena kuti, “Ulemerero, ulemerero, ulemerero”...Musati muzimuyesa Mulungu kuti muyankhule mu malirime, zingoulolani Mzimu kuyankhula kudzera mwa inu. Mukuona?

142 Tsopano, ine sindimakhulupirira mu kumuyesa Mulungu kapena kukankha chirichonse. Monga momwe ine ndinanenera kanthawi kapitako, pamene Mzimu...Ife timayembekezera pa Mzimu; Iwo umazichita izo.

143 Tsopano penyani, Paulo anali akutola nkhuhi pa chisumbu cha Krete, ine ndikukhulupirira apo panali. Ndipo iye anali mu unyolo, ndipo njoka, mwinamwake mamba...Kumeneko ndi kuluma kwa imfa; iye akanati agwere panso mofulumira kumene, wakufa. Ine sindikudziwa njoka ina iliyonse imene ingakuphe iwe mwamsanga chotero, kupatula iyo itakhala ili mamba.

144 Ndipo kotero iye anainyamula mamba iyi, ife tingoti. Iyo ndi yoluma mwakupha; iwe umangotsala ndi pafupi, kupuma pang’ono kokha kotsalira. Pamene mamba akugogoda iwe... Kapena mphiri, iwe umakhala ndi mwayi watheka kwatheka, ndi mankhwala, kuti ukhale moyo, ndi mphiri yakuda. Ndi mphiri yachikasu iwe umakhala ndi pafupi mwayi eyite pa zana kuti ufa ndi pafupi twente pa zana kuti ukhala moyo; mamba, iwe ulibe gawo lililonse. Iwe umakhala wakufa basi, ndizo zonse, chifukwa iwe sumapuma koma kupuma pang’ono kokha. Iyo imapangitsa zanzi misempha yonse, kayendedwe ka magari konse, ndi chinthu china chirichonse, ndipo iwe wapita. Mukuona?

145 Koma p—pamene mamba uyu amene anamuluma Paulo pa dzanja, iwo anati, “Chabwino, bambo ameneyo ndi... Iye ndi bambo woipa, mwinamwake wakupha. Ngakhale iye anapuluma pa nyanja, komabe...iye sakanatha kuithawa imfa. Milungu ikuti imubwezere iye monga chonchi—pokhala wakupha.”

146 Paulo anayang’ana, ndipo njoka iyi ikulendewera pa dzanja lake, iye anangoikutumula iyo nichoka, opanda kutengeka nkomwe, “O, Ambuye, ndithandizeni ine kuchita izi.” Ayi! Iye anayang’ana pa iyo, anaikutumulira iyo pa moto, anapitirira nazo kumatola nkhuhi ngati kuti palibe chimene chinachitika.

Iwo anati, “Iye afa mu miniti yokha, chifukwa pamene njoka imeneyo ikuluma iwe, iwe wapita.” Pambuyo pa kanthawi kapang’ono katapita, Paulo sanatupe, kufa, kapena palibe chochitika. Iwo anati...Iwo anasintha, anati, “Iyeyu ndi

mulungu amene watsika pansi mu mawonekedwe a munthu.” Mukuona?

<sup>147</sup> Iye sanati, “Ndibweretsereni ine njoka imeneyo,” koma njokayo inamuluma iye. Iye sanamuyese konse Mulungu, koma anali nacho chikhulupiriro mwa Mulungu kuti akhoza kugonjetsa kuluma kwa njoka. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>148</sup> Kotero aliyense yemwe inu muli pakati pa anthu ogwira njoka, i . . . Tsopano, ngati iwo akufuna kuti azigwira njoka, zimenezo ziri kwa iwo. Mukuona? Ine sindikuziwona basi izo mwa kachitidwe kameneko.

<sup>149</sup> Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, anthu amenewo ali nacho chikhulupiriro.” Ine sindikunena kuti iwo alibe chikhulupiriro, kudziyatsa okha ndi miuni ya acetelini ndi zinthu monga choncho, koma (inu mukuona?) komabe zimenezo sizikutsimikizira Mulungu.

<sup>150</sup> Ine ndawaonapo Amwenye akutenga—chingwe cha moto, chokandapala mapazi atatu ndi pafupi utali wa mayadi forte, pamene icho chimakupizidwa ndi masamba mpaka chimatentha kufika poyera (osati munthu wapadera, alimi), amavula nsapato zawo, amatenga pang’ono (ansembe kuwadalitsa iwo ndi magazi a mbuzi), ndi kutenga mbeza zazing’ono za nsomba, ndi kuzibaitsa izo mu khungu lawo cha pakamwa pawo, kufikira iwo atakhala chisokonezeko chimodzi chachikulu ch—cha madzi, atadzazitsa mu timipira ta ngati ta pa mtengo wa Khrisimasi monga choncho, zokongoletsera, atadizazitsa ito, ndipo mbeza zazikulu za nsomba zazitali choncho zitabaidwa mu mnofu wao (inu mungati mulingalire chomwe izo ziri kuzilowetsa izo umo ndi kuzitulutsa), ndi kuima monga choncho, ndi kumayenda kumene kudutsa pa moto wotentha uwo (ndipo iwo basi—utatentha moyera, kupyola pa kufiira ukutentha moyera)—kumayenda basi kudutsa mu moto umenewo ndi kutembenuka apo pomwe ndi kuyenda chobwerera, popanda ngakhale kuwawuka pa mapazi awo. Ndipo iwo samakhulupirira ngakhale mwa Mulungu wathu. Iwo amapembedza, kupembedza kwa ziwanda. Mukuona? Kotero izo sizikutanthauza chirichonse. Zingokhalani patali . . . Inu muzingokhala Mkristu weniweni, wokoma, ndi wodzichepetsa, zikhalani moyowo, ndiyeno Mulungu azisamalira zina zonse izo.

**419. M’bale Branham, azilaliki azilalikira pa chiani—azilalikira pa chiani amene sakupita mwa Mkwatibwi? Uthenga wawo tsopano, Mzimu Woyera, ubatizo wa mmadzi, ndi chipulumutso, iwo azidzalalikira chiani ngati iwo sapita mwa Mkwatibwi?**

<sup>151</sup> Chabwino, iwo adza . . . Inu mukudziwa chimene mwinamwake chiti chidzachitike? Ine ndikunena izi, tsopano. Ine sindingati nditsimikizire izi, koma i . . . Iwo mophweka

azidzapitirira nazo kumalalikira basi momwe iwo akuchitiramu tsopano, ndipo anthu nkumapitirira nazo akuganiza kuti iwo ali nkupulumutsidwa; ndipo Mkwatibwi adzakhala atapita kale.

**420. Kodi ndi zolondola, molingana ndi Mawu kumapanga za kuteteza kubala?**

<sup>152</sup> Ine ndinakuuzani inu kuti ine ndingayankhe zimenezo mwatokha. Inu amene muli ndi mafunso amenewa, bwerani kwa ine patokha.

**Wokonedwa M'bale Branham, ife tiri naye mphunzitsi amene inu mumamudziwa kuti Lemba limati . . .**

Eya, ine ndinali nalo limenelo. Miniti yokha tsopano.

**M'bale Branham, pa nthawi ina ife tinali nalo dzina lathu litalembedwa mu bukhu la winawake . . .**

Eya, ine ndinali nalo limenelo. Ilo nla momwe iwo analichotsera ilo tsopano, kodi iwo anachita cholakwika?

**421. Bwanji . . . Kodi inu mungavomereze kuteteza kubala?**

<sup>153</sup> Ayi, ine sindingavomereze iko. Ayi, bwana! Mwaona?

**422. Kodi . . . Kodi mngelo wachisanu ndi chiwiri, monga anayankhulidwa, wa Chivumbulutso 10, munthu yemweyo monga Eliya wa Malaki 4?**

Kodi ine ndinaliyankha limenelo? Limenelo silikumveka ngati ine ndinaliyankha.

<sup>154</sup> Inde, ndi munthu yemweyo. Chivumbulutso 10 ndi Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, amene . . . mtumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri wa M'badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri, amene ali Malaki 4.

**Kodi kuteteza kubala . . .**

<sup>155</sup> Ine ndiri nazo zambiri pa zimenezo. Ine ndinangoziponyera izi mmbuyo, ndipo i—ine sindimafuna kuti ndiziyankhe; ine ndingati bola ndikuwoneni inu mwatokha.

**423. Ndi pati pamene ife timapeza pamene Nowa analalikira kwa zaka handiredi ndi twente ndipo anamanga chombo mu zaka handiredi ndi twente?**

Kodi ine ndinaliyankha limenelo?

<sup>156</sup> Kam'badwo, kapena nthawi yoikidwa, nthawi yoikidwa ya munthu pa dziko lapansi inali zaka 120, imene inamutengera Nowa, nthawi, yoti amange chombo, imene inali kutengedwa ngati kam'badwo mu tsiku limenelo. Zaka wani handiredi ndi twente inali nthawi yopatsidwa kwa munthu. Ndipo iye analalikira, molingana ndi . . . Genesis 6:3, iye analalikira kwa kam'badwo kameneko, zimene zinali zaka 120; Nowa anatero nazo. Chabwino. Tiyeni tiwone tsopano.

**424. Mu Malaki 4, Eliya uyu ndi woti atengere mitima ya atate kwa ana, kenako mitima ya ana kwa atate. Kodi uyu ndi munthu yemweyo?**

<sup>157</sup> Inde, munthu yemweyo. Chabwino. O, dikirani miniti. Ayi! Ndikhululukireni ine, ine ndikupepesa. Basi. . . Mwaona Mzimu Woyera unandigwirira ine chimenecho apo? Ayi! Ine ndimaganiza kuti izo zinati. . . Mwawona?

<sup>158</sup> Chimene chinali mu Malaki 3, apo, “Ine ndidzatumiza mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga,” amene anali Eliya. Mu Malaki 4 zikutembenukira mmbuyo mozungulira ndipo anati, “Taonani ine ndidzatumiza Eliya.” Malaki 3, Iye anali woti amutenga mtumiki amutumize patsogolo pa nkhope ya Ambuye Yesu, amene anali Yohane. Ndi angati akumvetsa zimenezo? Malaki 4, pamene Eliya uyu abwera, nthawi yomweyo ukatha Uthenga wake ndi zinthu, ndi pambuyo pake, ndiko Kudza kwa Ambuye ndi kusinthidwa kwa dziko lapansi.

<sup>159</sup> Ndipo inu zindikirani, kuti tipangitse izi kutsimikizira tsopano kuti si. . . Momwe Mzimu Woyera unalemba izi ndi mneneri uyu, Iye anati, “Iye adzatembenezira mitima ya atate, poyamba, kwa ana.” Mukuona? Kumeneko kunali kubwera koyamba kwa Yohane. Iye anatembenzira mitima ya makolo, akale, makolo aumbadwa, kupita ku Uthenga wa ana, amene anali kambadwo katsopano apo, Yesu, mu kambadwo kameneko. Ndiye *ndi*, cholumukizira, icho chikumangiriza palimodzi “mitima ya ana kubwerera kwa makolo,” chimene chikutanthauza, Uthenga wa lero utembenezira mitima ya ana mu m’badwo wa mpingowu kubwerera ku chikhulupiriro choyambirira Chachipentekoste chapachiyambi.

<sup>160</sup> Kotero iwo adzakhala ali awiri osiyana. . . Mthenga mmodzi, koma izo zikusiyantsa pamenepo—kudza koyamba ndi kudza kwachiwiri, kwa Yohane. . . kapena mtumikiyo, Eliya.

**Mwamuna wanga ndi mwana wanga wamwamuna wamng’ono kwambiri sali kukhulupirira. . .**

Eya, ine ndinali nalo limenelo. Ine ndikudziwa ine ndinatero, chifukwa ine ndikumudziwa munthuyo walembe maina awo pamenepo. Ine ndikukumbukira ndimayankhula kwa iwo pambuyo pake pa zimenezo.

**425. Kodi ife tingachipeze bwanji chifuniro cha Ambuye? Pathu—pakhomo pathu. . . Kodi ife tisamutsire nyumba yathu ku Jeffersonville, Indiana? Kodi munthu angakhale Mkhristu ndi kusamawakonda anthu achikuda? Kodi Mulungu samafuna kuti iwo kuti azichitiridwa monga ife, chifukwa iwo ndi akuda mwa khungu? Kodi. . . Kodi inu lingaliro lanu ndi chiyani pa izi? Kodi inu mumakhulupirira mu kusakanikirana kapena kusankhana?**



<sup>161</sup> Ine ndimakhulupirira mu kusakanikirana. Ine ndimakhulupirira kuti munthu...Ziribe kanthu chomwe mtundu wake uli kapena yemwe iye ali, iye ndi munthu monga momwe ine ndiriri. Ndizo ndendende. Ndipo ine ndikukhulupirira, ngati iwo atangowasiya anthu achikuda amenewo okha, ndipo achikominisi awo akanati asapite kumeneko ndi kukawadzoza iwo. . .

<sup>162</sup> Tsopano, iwo ankafuna. . .Tsopano, anthu enieni achikuda, pali gulu lenileni lobadwa mwatsopano, anthu oyera mwaumulungu mwa anthu amenewo. Inde, ndithudi. Kungoti chifukwa thupi langa ndi loyera ndipo lawo ndi lakuda, izo sizikutanthauza kanthu kamodzi kwa ine. Iye ndi m'bale wanga ngati iye ali mwa Khristu.

<sup>163</sup> Ndi chifukwa chake ine ndimatsutsana ndi uthenga wa Chiafrika; iwo sanali kukhulupirira ngakhale kuti anthu amenewo anali nayo solo. Ndi chimene chinandipangitsa ine kusakonedwa kumeneko. Ine ndinati, "Munthu ameneyo ndi munthu chimodzimodzi momwe ine ndiriri. Iye ali nawo ufulu kwa mwayi wofanana umene ine ndiri nawo. Khungu lake siliri kutanthauza kusiyana ayi kwa ine, kapena kwa munthu aliyense amene wabadwa kachiwiri mwa Mzimu wa Mulungu."

<sup>164</sup> Koma ine ndinati, "Ngati iwo akanawasiya anthu achikuda awo okha, iwo sakanati akhale ali odzozedwa chonchi." Ndipo ine ndikuchinena ichi kuchokera pa guwa ili. . .Ife tiri nawo anthu achikuda ambiri amene amabwera kuno. (Ine sindikuganiza kuti pali wina pano usikuuno.) Koma ife tiri nawo anthu achikuda ambiri amene amabwera kuno ku mpingo uno. M'bale, iwo ali olandiridwa monga wina aliyense aliri. Iwo ndi m'bale wanga ndi mlongo.

<sup>165</sup> Ndipo ena mwa anthu abwino kwambiri amene ine ndinayamba ndakomana nawo mmoyo wanga ndi ena a anthu achikuda amenewo. Ndiye pali ena a iwo amene ali zigawenga, ndendende basi monga anthu oyera, kapena anthu achikasu, kapena anthu abulauni. Inde, ndithudi.

<sup>166</sup> Tsopano, ine sindimakhulupirira mu maukwati osakanizikana. Ine ndimakhulupirira kuti munthu woyera asamakwatire msungwana wachikuda, kapena msungwana wachikuda kukwatiwa ndi mwamuna woyera, kapena wachikasu kukwatira wachikuda, kapena woyera, kapena a. . .ine ndimakhulupirira kuti abulauni, akuda, oyera, ndi mitundu ya anthu ili ngati munda wa maluwa wa Mulungu, ndipo ine sindimakhulupirira kuti iwo azisakanizidwa. Ine ndimakhulupirira kuti umo ndi momwe Mulungu anawapangira iwo, ndipo ine ndikukhulupirira kuti umo ndi momwe iwo ayenera kumakhalira ali.

<sup>167</sup> Chiani. . .Izo zimandipusitsa ine kuti ndinawona msungwana wina wokongola kwenikweni wachikuda, kamwana

kowoneka kaluntha, kokongola basi monga mkazi aliylene amene inu mungafune kuti mumuwone. . . Iye akufunira chiani kukwatiwa ndi mwamuna woyera ndi kukhala ndi ana achi mulatto? Nchiani chimene msungwana wachikuda waluntha akanafuna ndi chinthu chonga chimenecho? Ndi chifukwa kuti chinachake. . . chikomisi icho. . . Ndipo akanafuna motani—wabwino. . . b—b—bambo wachikuda kuti akwatire mkazi wachizungu ndi kukhala ndi ana achi mulatto?

<sup>168</sup> Ine sindimakhulupirira i. . . Ine ndikukhulupirira kuti inu muzikhala basi momwe ife tiriri. Ife—ndife antchito a Khristu. Ndipo Mulungu anandipanga ine. . . Ngati Iye akanandipanga ine, mtundu wanga wakuda, ine ndikanakhala wokondwa kukhala ndiri munthu wakuda kwa Mulungu. Ngati Iye akanandipanga ine wachikasu, ine ndikanakhala mwamuna wokondwa wachikasu kwa Khristu. Ngati Iye akanandipanga ine woyera, ine nkanakhala. . . ? . . . munthu woyera wokondwa kwa Khristu. Ngati Iye akanandipanga ine wabulauni, kapena wofiira, Mmwenye, chirichonse chimene chiri, ine ndikanakhala mtundu wa khungu langa womweo. Ameneyo ndikanakhala ine. Ine ndikufuna kukhala momwe Wondipanga wanga anandipangira ine.

<sup>169</sup> Kumusi uko tsiku lijali mu Shreveport pamene kuwukira kuja kunabwera, ndipo iwo. . . ndipo uko kunali achikuda achinyamata aja atadzedwa kumeneko, achikominsi. . .

<sup>170</sup> Ine ndinakuuzani inu pano pa guwa ili, Martin Luther King ndi chobwerekera chachikulu chimene anthu achikuda anayamba akhalapo nacho. Kulondola. Mwamuna ameneyo atsogolera zikwi za iwo kokaphedwa (ndiko kulondola), atadzedwa ndi chikominsi.

<sup>171</sup> Ndiroleni ine nditsimikizire nsonga yanga. Ine ndinanena izo pafupi zaka ziwiri zapitazo. Taonani zimene zikuchitika pakali pano. Iwo ankanena kuti iwo anali kumenyera kusakanizikana, ndipo pamene lamulo linawapatsa iwo kusakanizikana. . . Ndipo kwa inu anthu amene simumakhulupirira mu kusakanizikana, ndikuchita nanu manyazi. Fuko lathu limaloleza kusakanizikana, ndipo ife tizichita zimene bwana wamkulu akuti tizichita. Ndizo ndendende kulondola.

Ndipo tsopano, inu mukuti. . . Asati azibwera mu malo, ndi zina zotero monga choncho, kapena kugula, kapena kukhala kumbuyo kwa basi, ndi zina zotero, ayi, bwana! Lamulo linati iwo ali chimodzimodzi basi momwe ife tiriri, kotero ife tiri chimodzimodzi momwe iwo aliri; kotero tiyeni ife tizichita mwanjira imeneyo. Tiyeni ife tikhale mwanjira imeneyo. Ndipo ndizo ndendende zimene anthu onse obadwanso mwatsopano mowona amakhulupirira. Ndipo tsopano, ine ndikukhulupirira kuti izo ziri mu mtima wao.

172 Ine sindinayambe ndakhala ndi kumverera kotero kwa anthu monga ine ndiriri nako kwa anthu osauka awo mu Afrika, momwe iwo anali kuchitidwira. Ndipo ine sindimakhulupirira mu zinthu zimenezo. Ine ndine wakummwera; ine ndinabadwa kutsidya kwa mtsinjewu kutaliko, koma ine ndiri ngati Abraham Lincoln; ine ndinabwera kuno, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti anthu anabadwa mofanana. Ndiko kulondola. Ndipo ine sindimakhulupirira mu kulekanitsa anthu ndi zinthu monga choncho, pamene anthu amenewo... anabatizidwa ndi Mzimu Woyera ndi zina zotero.

173 Koma taonani, si anthu achikuda enieni awo Akhristu obadwa mwatsopano amene akuyambitsa vuto lonseli. Inu mukufuna kuti muwaweruze iwo chifukwa cha izo, nanga bwanji zigawenga zathu ana oyerawa? Mukuona? Tsopano, msuzi wa tsekwe wamphongo ndi wabwino monga wa tsekwe wamkazi. Bwanji, ana athu oyera amayambitsa mavuto pawiri kuchuluka kwake monga iwo amachitira. Ndizo ndendende kulondola. Kodi izo ziri kuti? Mu makoleji athu ndi zinthu monga izo. Ena a anthu athu ophunzira mwapamwamba akumayambitsa zinthu zimenezo. Mukuona?

174 Chabwino, ndi chiani icho? Tsopano, pofuna kuti ndikusonyezeni inu kuti ndi chikominisi ndipo osati anthu achikuda awo, ndi momwe chikominisi nthawizonse chimadzera kuti chidzalande. Iwo amachita zimenezo mu fuko lirilonse. Ndi momwe iwo amachitira izo, kukupangitsani inu kuti muzimenyana pakati pa wina ndi mzake, kuwukira, ndiye iwo amalilanda ilo popanda kuwombera. Iwo sakufuna kuti aliwombele dziko ili; iwo akulifuna ilo. Iwo akhoza kuika zomera zambozi mmenemo. Ndipo tsopano, iwo awona mlandu wa kuchita zimenezo, ndipo akudziwa chomwe kuwukira kwakale kunali, ndipo aganiza kuti iwo angayambe kuwukira kwina.

175 Kuti nditsimikizire nsonga yanga kuti ndi yomveka, iwo atakhala nako kale kulowererana (iwo ali nako iko tsopano, mololezedwa, mwalamulo), iwo akuyambitsa vuto lochuluka tsopano kuposa momwe iwo ankachitira pa malo oyamba. Mukuona? Izo zikusonyeza kuti ndi chikominisi ndipo osati miyoyo yofunika iyo imene inabadwa mwa Mzimu wa Mulungu.

**426. Kodi ife tikhalebe pamoto ndi kumalalikira Uthenga, kapena nthawi yatha?**

176 Ayi, pitirirani kulalikira molimba basi monga momwe inu mungalalikirire. M'bale, khalani nawo iwo; ine ndiri kumbuyo kwanu komwe.

**427. M'bale Branham, pamene inu munanenera za: osamadya mazira, osamakhala mu chigwa, kodi umenewo unali uneneri wa inu nokha kapena kwa osonkhana? Chabwino.**

177 Zaka zapitazo, pafupi zaka sate zapitazo, ine ndinapereka uneneri kuti zidzafika pochitika mu masiku otsiriza kuti kudzakhala kuli matenda pakati pa zinyama, pakati pa ng'ombe, ndi mazira, ngakhale kwa mazira. Ndipo zidzafika pochitika, kuti padzakhala mazira amene sakanakhala oyenera kumadyedwa. Ndiponso, izo zikanafika pochitika kuti anthu okhala mzigwa... Tsopano kumbukirani, ine ndinanenera zimenezo mmbuyo kwambiri zaka sate zapitazo, kuti izo zikanadzafika pochitika, kuti anthu okhala mzigwa, kuti ine ndinawapempha Akhristu kuti asamuke kuchoka mchigwa, ndipo kuti iwo asamadye... Nyama zosiyana ndi zinthu monga izo, zikanakhala ziri ndi chiphe. Izo zikanakhala ziri zoopsyia (ine ndikukhulupirira momwe ine ndinaliri nazo izo) kuti anthu azikhala mzigwa.

178 Tsopano, izo zinali iwo asanakhale ndi zolakatika kapena iwo asanadziwe chirichonse cha zolakatika. Koma umenewo unali Mzimu Woyera ukundichenjeza ine. Ndipo pakali pano, ngakhale kwa ng'ombe zathu (inu mukuziwona izo zikuchotsedwa pa msika) zikumapemereredwa ndi DDT amene wakhazikitsa chinachake mwa ng'ombezo.

179 Zindikirani kachiwiri, zonse izi zopanga haibridi zinthu ndi zinthu zimene iwo akuzichita mwamtheradi zikuvunditsa mtundu wa anthu. "Sate pa zana," twente kapena sate pa zana, *Reader's Digest* inati, "odwala mu chipatala akuyikidwa mmenemo chifukwa cha madokotala." Iwo amakupatsani inu mankhwala kuti achotse izi mwa inu, ndipo iwo amayika chinachakenso mmenemo.

180 Ndipo kodi inu munazindikira mazira? Chaka chatha nkhani mazana mu Louisville ndi Jeffersonville anayamba kudwala ndipo anaikidwa muchipatala chifukwa chosanza atadya mazira amene nkhuu za mu chigwa kuno... Mazira ochokera ku chigwa anatenga zolakatikazo. Ndi kuika chiphe mu zomera, ndi zina zotero, chirichonse chaipitsidwa.

181 Koma kuno ndi kumene inu mukuzipeza izo, m'bale wanga. Ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti zinalembedwa mu Lemba k—kuti palibe chakudya chiyenera kumalandiridwa popanda icho kulandiridwa ndi mathokozi, pakuti icho chimayeretsedwa nao Mawu a Mulungu ndi pemphero. Mukuona? Ngati inu muzidya icho, muziti, "Ambuye Yesu, Inu mwandikonzera ine chakudyachi. Tsopano, ndi chikhulupiriro ine ndikuchiyeretsa chakudya ichi kuti chipereke mphamvu kwa matupi athu." Ndiye mkuchidya icho, pakuti mu zonse zimene ife timachita ziri mwa chikhulupiriro.

**Wokonedwa M'bale Branham, choyenera cha chilekano kwa mwamuna woledzera?**

<sup>182</sup> I—ine sindikukonda kuyankhula za chilekano izo. I—izo. . . Izo, i—i—ine ndidzayankhula za zimenezo kanthawi kena mtsogolo.

**428. M'bale Branham, M'bale** (Miniti chabe. Izi ndi zokhudza mmodzi wa atumiki pano. Ndisiyeni ine ndiwerenge izo poyamba. [M'bale Branham aimikira ndi kuwerenga funsolo kwa iyemwini—Mkonzi.] Nhu! Miniti chabe. Chabwino, ine ndikuuzani inu. Ine ndiliwerenga ilo mulimonse.)—**M'bale Branham, M'bale Neville anandiuza ine kudzera mu ulosi kuti PAKUTI ATERO AMBUYE kuti ine ndikanati ndilandire Mzimu Woyera. Anandiuza ine ndi chitsimikizo ichi kuti ine ndikanati ndilandire Mzimu Woyera, ine sindinatero mpaka pano kulandira Mzimu Woyerawo. Kodi ine ndizipitiriza. . .**

<sup>183</sup> Inde, ndithudi! Zichitani zimenezo. Pitirizani nazo kukhulupirira.

Zindikirani, ine kuitana. . . ndinali nditaima kwa M'bale Wood dzulo pamene kuitana kwa foni kunabwera kuchokera kwa bambo amene ali mu chikuku, amene anabwera kuno atapsyinjika chifukwa cha m'bale kapena winawake amene a—amene anali chidakhwa ndipo wakhala atapita kwa Othandizira ndi kubaidwa, mu chipatala, ndi zina zotero; ndipo M'bale Neville, poyankhula mu malirime kapena mwanjira ina anapereka—ulosi pa munthu ameneyu, ndipo anapereka ulosi kuti chinachake chikanati chidzachitike kwa bambo ameneyo kwa ubwino mkati mwa masiku pang'ono otsatira, kapena chinachake chonga icho. Ndipo bamboyo anabwera kuno ndipo ananena kuti bambo uyu, masiku sikisite—eyiti tsopano, wakhala atachokera ku chipatala, sanamwe chakumwa chimodzi, kapena kumwa mankhwala amodzi omupangitsa kuti asamwenso, kapena chirichonse. Ndipo chinthu chimene M'bale Neville ananena mu ulosi chinafika pochitika. Ambuye alemekezeke! Ife tikumukhulupirira m'bale wathu kuti ndi munthu wa Mulungu.

### **Wokonedwa M'bale Branham, kodi awo. . .**

<sup>184</sup> Tsopano tadikirani, ndiroleni ine ndiime pamenepo miniti yokha. Tsopano, izo ndi zimene ine ndikuyesera kuwauza anthu. M'bale Neville amakhulupirira Uthenga womwewu umene ine ndikuukhulupirira. M'bale Capps, M'bale Beeler, M'bale Ruddell, abale onse awa ozungulira kuno akukhulupirira Uthenga womwewo umene ine ndikuukhulupirira; iwo amawulalikira Iwo, momwe ine ndimachitira.

<sup>185</sup> Ndipo ngati inu mukufuna, mukufuna kwenikweni kutero, inu mukuyenera kupita kwina, ndipo inu mukuti mupume kapena chinachake kapena chimzake, ndipo mukufuna kubwera chifukwa cha Mawu, bwerani kuno. Bwerani ku kachisiyu, ndi kumene inu muziwumva Iwo.

<sup>186</sup> Awa ndi amuna aumulungu. Iwo ndi amuna amene ali ndi Mzimu Woyera womwewo umene ine ndiri nawo n—ndipo inu muli nao, amaphunzitsa kuchokera ku Baibulo lomwelo ndi Uthenga womwewu.

**Wokonedwa M'bale Branham, kodi iwo amene azidzayankhula mu malirime ali mu otsalira. . .**

Eya, ine ndinali nalo limenelo. Nhu, nhu, ine ndinali nazo zimenezo. Anabadwa akuyankhula mu malirime.

**M'bale Branham, ulaliki wanu pa ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi ubatizo mu Dzina la Yesu. . .**

Eya, ine ndinali nalo limenelo. Tiyeni tiwone.

**429. M'bale Branham, Baibulo limatiuza ife kuti m—mkazi azimvera mwamuna wake. Ine ndine Mkhristu ndipo mwamuna wanga ndi wochimwa. Iye amandizunza ine mwanjira iliyonse imene iye angathe, ndi kuti ine ndisamapite ku tchalitchi, ndi kuwerenga Baibulo langa, n—ndipo akuwakana Mawu. Kodi ine ndichite chiyani?**

<sup>187</sup> Kodi inu muchite chiyani? Tsopano, mvetserani, inu mukuyenera kuti muzimumvera mwamuna wanu; amenewo ndiwo Mawu. Tsopano, ngati iye akukuuzani inu ndi kukukanizani inu kuwerenga Baibulo, kupita ku tchalitchi, kapena chinachake monga izo, inu simukuyenera kuti mumvere zimenezo, chifukwa, “Iye amene s—sadzasiya bambo ake, amake, mwamuna wake, mkazake, kapena aliyense amene ali ndi kunditsatira Ine, sali woyenera kukhala Wanga.” Ndi kulondola uko?

<sup>188</sup> Ayi, musatero. . .Mwamunayo akuyenera. . .inu simuli. . . Mwamuna sayenera kugwiritsa ntchito ulumuliro woterowo pa mkazi basi chifukwa chakuti iye ndi womulamulira wake. Mulungu ndi womulamulira wake pamwamba pa inu, m'bale. Mwawona? Ndipo ngati mkazi wanu akuchita chinachake cholakwika, ndiye musatero. . .ndiye inu muli nawo ufulu womuuza iye, ndipo iye akuyenera kuti azikumverani inu. Koma inu mulibe ufulu woti muzimumenya iye, kapena kumamukhwekhwereza iye uko, k—kapena kumachita zinthu zimenezo. Ayi! Iye. . .

<sup>189</sup> Mulungu anamupangira mwamuna womuthandizira, osati chopondera pakhomo. Kumbukirani, i. . .Iye anali wapamtima wanu; iye nthawizonse azikhala chimenecho.

**430. Nliti ndi kuti kumene anthu a Mulungu adzasonkhanire kuti alandire Mawu Otsiriza?**

<sup>190</sup> Mwa Khristu. Inde! Kwa tsiku lotsiriza, iwo adzasonkhana mwa Khristu. Musati muiwale zimenezo tsopano. Ife tiri nawo malo osonkhaniranamo; ife tiri nawo iwo ndendende basi.

**431. Ife tikutchedwa. . .(Tsopano, ili ndi funso la tsiku lina lija.) Ife tikutchedwa mbalame zodetsedwa, chifukwa**

**ife timapita ku mpingo wa Junior Jackson. Nthawizina chifukwa ife timakhala ndi—i...Iye samachita mwa malamulo atsopano a mpingo kuno pa mpingopa. Kodi ife tiri kunjwa kwa chifuniro changwirowo cha Mulungu tikanamasonkhana kumeneko nthawi zina?**

191 Ayi, bwana! Ine ndikukhulupirira Junior Jackson kuti ndi mwamuna wa Mulungu. Ine ndalongosola kale zimenezo. Ine ndikukhulupirira...

192 Tsopano, ife sitimagwirizana pa dongosolo la mpingo. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti Junior—Junior...Bwanji iye...Ndi angati amene akumudziwa Junior Jackson? Bwanji, ife tikudziwa kuti mwamuna ameneyo ndi mwamuna waumulungu. Iye amakhulupirira Uthenga uwu chimodzimidzi basi momwe ine ndikuchitira, ndipo iye amakhulupirira zinthu zimenezi. Kunena moona, Junior ndi ine ndife abwenzi basi, monga ngati amuna ena onse awa kuno, J. T., n—ndi M'bale Rudell, ndi M'bale Jackson, ndi M'bale Beeler, ndi ena onse abale awa pano; tonse ife, ife tiri limodzi. Tsopano, ife sitiri...tikhoza kusamawonana basi diso kwa diso mofanana (mwawona?), koma ife tikukhulupirira Uthenga wofanana (mwawona?), ndipo ife tikumamatirana palimodzi. Pali M'bale Hume uko nayenso, mtumwi, ndipo o, ambiri osiyanasiyana, i...Nthawizina ine sindimakwanitsa ngakhale kuwatchula maina awo, koma i—inu mukudziwa ine ndikutanthauza inu mulimonse, m'bale. Zedi.

**Inu mukufuna kusiya kuchita zaunamwino...**

193 Ine ndinafunsa zimenezo. Mukukumbukira? Ndi mlongo wokoma wokondedwa amene amafuna kudziwa za kuchita unamwino.

**Pamene ine ndinali wamng'ono, ine ndinali... ndinkamuuzwa aliyanse kuti ine ndimafuna kuti ndikhale mlaliki. (Ine ndinali nalo ilo. Ine ndiri nalo ilo aponso.) Ndiye kodi iye azichita chiyani pa izo lero?**

194 Chabwino, iyi ndi kalata yochokera kwa—mtumiki wantchito wa Khristu, iyo si ili...Iyo ndi kalata ya ndekha kwa ine. Iyo ndi yochokera kwa M'bale Pat Tyler, mmodzi wa abale athu kuno ku mpingowu.

Ndiwo onse a iwo. Tithokoze Ambuye. Ine ndikuyamikira kwa inu anthu. Ine ndangotenga...[Kagawo kakusowa pa tepi—Mkonzi.]

...ndi amodzi,  
Zitonthozo ndi chisamaliro chathu.

195 Ndikudabwa ngati Mlongo Wilson akadali mu nyumba ino? Ine ndinamuwona iye muno. Inu mukudziwa zimene ine ndimachita kanthawi kapitako, Mlongo Wilson? Ine ndimayang'ana pa zithunzi pamene ife tinkayika mwala wapangodya. Ine ndimayang'ana pa chithunzi ndipo

ndinamuwona Hope ndi ine ife tisanakwatirane. Ine sindimadziwa nkomwe izo. . . Ine ndikukumbukira ndinawona chithunzi pamene ine ndinkatuluka kuchokera mu imodzi ya nkhonya zanga, pamene ine ndinapambana ukatswiri. Ndinayang'ana pa chithunzi changa usiku wina pamene ine ndinali wolondera zinyama kuno mu Indiana. Ndipo ine ndikuganiza za mpingo. Inu mukudziwa, ine ndikupenekera kuti palibe kupatula pafupi munthu mmodzi wakhala pano usikuuno kuchokera mu gulu limenelo amene watsalira. Ndi angati ali muno kuyambira pa nthawi imene ife tinkayika mwana wapangodya kumbuyo uko pachiyambi? Kwezani dzanja lanu.

<sup>196</sup> M'bale wanga, Mlongo Wilson, ine ndikufuna inu—kuti ndikufunsi inu awiri chinachake. Mukukumbukira momwe ife tonse tinayambira? Mukukumbukira pansi pakale pamene iyo yonse inali itadzaza ndi matope? Tinali ndi mazenera akale amene ankagwadera. Ife tinali ndi masenti eyite oti tiyambire nao. Mulu wawukulu wa zomera, ponse apa inali nkhalango monga kumbuyo kwathuku pano pamene ife tinkamumanga iye, kachisiyu.

<sup>197</sup> Kuyang'ana pa tonse a ife amene tinatenga malumbiro athu ndi kuyenda tikuzungulira guwali. Ife tawawona iwo akubwera ndi kupita, wina kuchokera kwa wina. Kodi inu mwazindikira iwo amene akhala nao Uthenga, momwe iwo anapitira? Tsopano, ganizani za iwo amene anachoka ku Uthengawu, momwe iwo anapitira. Ganizani za izo.

<sup>198</sup> Ife tiri pano usikuuno, pambuyo pa gulu lonse lija la katatu kwa limene ife tiri nalo pano pa misonkhano yathu yodzazitsa. Taganizani za zimenezo, pamene mabasi a sukula anali kuimikidwa konse pa dziko lomweli kuno kuchokera konse kozungulira kulikonse, chokwera ndi chotsika kudutsa mu malo awa. Ngakhale osefukira mu mahema atakhala kunja uko kuti tiwasamalire iwo, ndipo komabe iwe unkalephera kuti uwakhazike anthuwo penapake, titasonkhana palimodzi. Ine ndinali ndiri mlaliki wamng'ono chabe. Mukuona? Ndipo kuchokera mu zikwi zimenezo zimene ife tinali nazo, pali atatu a ife tatsalira muno usikuuno.

<sup>199</sup> Ine ndikukumbukira Mlongo Wilson uko pamene ine ndinaitanidwa pambali pa bedi yake akufa ndi T.B., akuwukha magari, mpaka zofunda ndi zotsamira zinali ziri, zamagazi, pa ngodya. Ine ndikukumbukira Mzimu Woyera utaimitsa magariwo. Masiku pang'ono pambuyo pake ine ndinamubatiza iye mu Mtsinje wa Ohio mmadzi achisanu mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo ndinamukhazika iye kumbuyo kwa galimoto langa lotseguka, roadster yaing'ono yachikale, ndi kumunyamula iye kuchokera ku Utica. . . Kodi izo si zoono? Kuchokera. . . [Mlongo Wilson ayankhula kwa M'bale Branham—Mkonzi.] Eya! Mlongo Hope, mkazi wanga, mlongo



apo, anali pa mpando wakutsogolo wa roadster yaing'onoyo, ndipo amayi anga ndi Mlongo Snelling kumbuyo kwake. Ine ndiri nacho chithunzi chawo, Mlongo Snelling, Amayi, ndi onse, Akazi a Weber, Akazi a . . . apongozi anga aakazi, tonse ife kumusi uko, ndi Meda, ali kamtsikana kakang'ono chabe katayima pamenepo, ndipo tsopano, mzimai wa mutu waimvi. [Mlongo ayankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi.]

<sup>200</sup> Ine ndikukumbukira pamene iwo anali ndi tsiku la komata kakang'ono kuti tipeze ndalama zathu zoyambirira. Ndipo ine ndikukumbukira Hope atayima pa ngodya, anali ali msungwana chabe, pafupi sikisitini; anali akugulitsa monga chonchi, atanyamula komata aka apo. Akumawapatsa iwo komata. Iwe umakhoza kuika umo . . .

Woledzera anabwera uko mu msewu; iye anati, “Ndikhululukire ine, Abiti!” Anati, “Kodi iwe ukugulitsa chiyani?”

Anati, “Palibe. Kuti ine ndikupatseni komata aka.” Anati, “Ndi chopereka cha tchalitchi. Ngati inu mukufuna kuti muyike chirichonse umu ngati chopereka, ife tikuyesera kuti tipeze ndalama zokwanira zoti timangire kachisi wa . . . mu mzindawu.” Anati, “Ngati inu mukufuna kuti muyikemo chirichonse, inu mukhoza, koma ngati . . .”

Anati, “Ine ndiribe kalikonse.”

Anati, “Tengani komataka mulimonse.” Iye anatenga ndipo anayang'ana pa iko. Ku mbali imodzi an—an—anati, “Kodi inu mukakhala kuti mu Umuyaya?” Ndipo ku mbali inayo kunali chizindikiro chofunsira. “Kodi inu mukakhala kuti mu Umuyaya? Funso.”

Iye anazandimira mmbuyo, anayang'ana pa iko; iye anati, “Abiti, iwe ukufunsa funso lovuta!”

Iye anati, “Koma ilo liyenera kuyankhidwa!” Ndiko kulondola. Iye anapita kale kuseri kwa katani usikuuno. Ine ndikukumbukira mawu otsiriza amene iye anawanena. Ine ndikukumbukira zimene ine ndinamuza iye; ine ndikuzikumbukira izo. Inde, bwana!

<sup>201</sup> Madzi ambiri apita pansa pa mtsinjewu. Ife tinkakonda kuima pansipa . . . Ndipo ife tisanakhale nkomwe ndi tchalitchi, ife tinkakonda kuima ndi kugwirana manja ndi kumaimba nyimbo iyi kuno. Ine ndikukhoza kuimva iyo chabe. Myrtle anali kamwana kakang'ono kwambiri pamenepo. Ine ndiri ndi chithunzi cha Leroy wamng'ono ataima kumeneko, basi ali kamwana kakang'ono ngati.

Chodala ndi chimango  
Mu chikondi cha Chikristu;  
Chiyanjano cha apaubale  
Chonga chakumwamba.

202 Pamene ife tikuimba imeneyo pali ochuluka a iwo akuyembekezera kutaliko kudza Kwake.

. . . ife tikamasiyana,  
 Zimatipatsa kupweteka; (Kodi inu  
 mukukondana wina ndi mzake monga  
 choncho?)  
 Koma tikhalabe olumikizana,  
 Kuyembekeza kudzakomananso.

203 M'bale Freeman, inu mwayandikira kwa zimenezo, sichochu inu? Ine ndimangoganiza, ine ndinakudziwani inu pamene ife tinapita kwa M'bale Roy. Inu mukuwakumbukira a Adcocks? Ine ndiri ndi Kenneth. Kodi dzina la mlongo wake anali ndani? [M'bale Freeman ayankhula kwa M'bale Branham—Mkonzi.] Ine ndiri ndi naman chithunzi chawo; ife tonse tinali titaima pamenepo ndi mikono yathu titakumbatirana wina ndi mzake, titazungulira kutsogolo kwa malowo, Dr. Roy E. Davis, m'busa. Ine ndinali kuyang'ana pa iwo kanthawi kapitako. Doc anandibweretsera zithunzi zakalezo kuno. Zinakhala ngati zinandipangitsa ine kumverera mwachirendo kwenikweni pansi apo. Tsopano izo. . . ambiri a iwo anapita kale (mwawona?)—apita kale. Sizikhala motalika mpakana tidzakhala ife titapita kale. Mwawona? Koma. . .

Koma pamene tisiyana,  
 Zimatipatsa kupweteka;  
 Koma tikhalabe olumikizana,  
 Kuyembekeza kudzakomananso.

204 Kodi inu mukumukumbukira M'bale Bosworth? Asanawoloke kumene, iye anauka mu chipindacho, anayenda chodutsa pansipo, ndipo anagwirana chanza ndi bambo ake, amake, ndi owatembenezira ake kwa Khristu. Zaka forte, anali atafa zaka forte kapena fifite. Iye ankawawona iwo ataima pamenepo mu chipindacho, akuyesera kuti amufikitse aliyense poti awaone iwo. Kodi chinali chiyani icho? Bambo wokalambayo anali akuwolokera mu dziko limenelo kumene ine ndinali mu masomphenya mmawa uja. Ndiko kulondola.

205 Ine ndinawawona iwo kumeneko; iwo anali aang'ono kachiwiri. Ife tikanali olumikizana mu mtima; ife tikuyembekeza kuti tidzakomana kachiwiri. Uko nkulondola. Mulungu akudalitseni inu.

206 Ine ndinapezeka ndikuyang'ana mmbuyo mu nyumbayi, kukamba za amzanga achikuda, ndipo ine ndikuwaona M'bale ndi Mlango Nash atakhala kumbuyo uko. Ine sindimadziwa kuti inu munali kumeneko. Zinangopezeka kuti ndinayang'ana mmbuyo; iwo ali mmbuyo momwe. Ndipo m'bale wina uyu wakhala apa. . . Kodi uyo ndi m'bale uja amene amandipatsa ine kufuulira kwakukulu kuja kumbuyo uko kamodzi pa kanthawi, amene wakhala apayu? Ine sindikutha kuganzira

dzina lake. M'bale Wood amati iye anali kulankhula kwa iye. Iye anati, "Inu mukudziwa? Pamene Mzimu undikhudza ine, ine ndimayenera kufuula 'Eee!'" Anati, "Ine ndikuyembekeza kuti ine sindimasokoneza chirichonse." Pamene inu simumafuula "Ee!" izo zimandisokoneza ine. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndimakukondani inu m'bale, mlongo. Ndiko kulondola.

<sup>207</sup> M'bale Nash, Mlongo Nash, inu mukudziwa ine ndimakukondani inu. Inde, bwana! Inu ndinu m'bale wanga ndi mlongo mwa Khristu Yesu.

<sup>208</sup> Wokonededwa abwenzi okoma, ndi ena aliwonse, ngati ine ndaphonya ena a iwo, makomo amenewo ali otsegukira kuno kwa inu. Makomo akumwamba adzakhala ali otseguka nawonso.

Koma tikhala olumikizana,  
Kuyembekeza kudzakomananso.

Changa... *Chikhulupiriro Changa Chikuyang'ana*  
*Mmwamba kwa Inu*, tsopano, pamene ife tikuimba. Tiyeni kamodzi kenanso tiyimbe tsopano. Ndi nthawi yoti tizipita kwathu tsopano.

Chikhulupiriro changa kwa Inu,  
Mwanawankhosa waku Kalvare,  
Mpulumutsi waumulungu!  
Ndimveni ndipemphera,  
Chotsani machimo anga,  
Ndiroleni n'khale Wanu mwamphumphu!

Tiyeni tiyesere ija ya *Woyera, Woyera* kachiwiri, mungatero inu? Tipatseni ife mayimbidwe, Mlongo. "O..." Inu mukuidziwa iyo? Inu mukukumbukira pamene Mlongo Gertie ndi iwo anakakonda kuyiimba iyo?

<sup>209</sup> Tsiku likufa kumadzulo, Miyamba inadalitsa dziko lapansi; dziko lapansi ladalitsika. Momwe ine ndimakondera kulowa kwa dzuwa lamadzulo, likamapita pansu, mbalame zikupanga kuitana kwawo kotsiriza. Zimenezo ziyenera kuti zidzabwere kwa aliyense wa ife pamenepo. Ine ndikuganiza nthawi yamadzulo iyo... Kodi inu munayamba mwazindikira, mphepo idzasiya kuwomba; mbalame zidzakhala bata. Mukuona? Ndi dziko likufa, tsiku likufa kuti likabadwe kachiwiri mawa mmawa. Chabwino, tiyeni tiyesere iyo tsopano ngati ife tingathe.

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu  
Wamphamvu kwambiri.

Lee, tabwera kuno kwa miniti. I—i—ine ndikukhulupirira kuti i—ine sindikuganiza kuti ine ndikuidziwa iyo nkaimbidwe kameneko. Ndiroleni ine ndiyesere iyo popanda zing'wenyeng'wenye. Mukuona? Tiyeni tiwone ngati ife tingaipeze iyo. Tsopano, ine ndikudziwa...ine ndikhoza

kuilakwitsa iyo. Mukuona? Inu mundithandize ine tsopano, aliyense wa inu, tsopano.

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu—  
wamakamu!

Kumwamba ndi dziko mwadzaza Inu;  
Kumwamba ndi dziko zikupembedzani,  
Ambuye wammwamba mwamba! (Inu  
mukuikonda iyo? Kodi zimenezo sizikuchita  
chinachake kwa inu? Tiyeni tiyeesere iyo  
kachiwiri!)

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu  
wamakamu!

Kumwamba ndi dziko mwadzaza Inu;  
Kumwamba ndi dziko zikupembedzani,  
Ambuye wa mmwambamwamba!

<sup>210</sup> Ine ndikuikonda iyo, sichoncho inu? O, ine ndimangokonda nyimbo zachikale zimenezo. Pali chinachake pa nyimbo zimenezo chimene ine ndimachikonda. Inu mukhoza kukhala nazo nyimbo zanu zazing'ono zoduladula zimene inu mumazifuna. Ndipatseni ine zimenezo; ine ndimakonda zimenezo. *Kudutsa Chotchinga Chong'ambidwa*, nyimbo zina zonse izi zokongola monga choncho; ine ndimazikonda nyimbo zimenezo. Ine ndikuganiza kuimba ndi gawo la kupembedza (inde, bwana!), kuimba matamando kwa Ambuye.

<sup>211</sup> Chabwino, kwa yotibalalitsa yathu, tsopano, nyimbo, ndiyo *Tenga Dzina la Yesu Nawe*. Ambuye atakudalitsani inu tsopano pamene ife tikuimirira.

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wachisoni ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Litenge kulikonse upita.

Dzina lofunika, O kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, O kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba.

Tsopano iyi ndiyo ndime imene ine ndimaikonda, ndipo iyo ndi chenjezo kwa nonse a inu tsopano. Tizichita chiani?

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Chishango ku misampha yonse; (Mvetserani!)  
Mayesero akakuzungulira, (Uzichita chiani?)  
Zingopuma Dzina loyera mpemphero.

Dzina lofunika, O ndi kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba;

Dzina lofunika, O ndi kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

Mpaka tidzakomane, mpakana tidzakomane,  
Tidzakomane pa mapazi a Yesu; (Mpaka  
tidzakomane.)

Mpaka tidzakomane . . .

[Winawake ati, “Kodi mungandikumbukire ine mu pemphero?”—Mkonzi.] Ambuye Yesu, mudalitseni m’bale wanga wokondedwa, ndi kumuchiritsa iye tsopano mu Dzina la Yesu.



*Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo*, Bukhu Lachiwiri  
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume Two)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)